


# M'BADWO WA MPINGO

## WA SARDE

 ...mfumu. M'bale wanga amangondiuzza ine kuti panali mipango iyi, inali ya winawake yemwe akufa ndi khansa. Chotero ife tikhala tikuwapempherera iwo mkamphindi pang'ono. [M'bale Neville akuti, "Pali zopempha ziwiri pompo pa mbali inayo."—Mkonzi]. Zopempha ziwiri? Chabwino, ine nditero... ["Chimodzi cha izo. Chinacho ndi chopempha."] Chabwino, bwana. Ndipo ine ndiziika izo apa kuti ndizipempherenso izo.

<sup>2</sup> Ndiyeno winawake wangopereka cholembedwa, anabwera ndipo anadzapereka cholemba apo... cha misonkhano ya mawa. Inu amene mwabwera kuno kudzatichezera ife, ife ndithudi tidzakhala okondwa kukhala nanu mutabwera masana nthawi ya thuu koloko, mawa masana, iwo adzakhala ndi misonkhano ya tepi. Ndipo ngati inu simukuchita chirichonse, padzakhala umodzi wa mauthenga omwe—omwe inu simunayambe mwawamvapo adzakhala akuseweredwa ndi kudzakhala ndi msonkhano wa pemphero, ndipo—ndipo ife tikungoyembekeza nthawi yabwino mawa masana pa thuu koloko. Idzakhala nthawi yotangwanika kwambiri kwa ine chifukwa mawa, mwaona, ine ndidzayenera kudzatenga Lamlungu mmawa, ndiponso Lamlungu usiku, ndi mawa usiku, aponso, ndi mbiriyakale yonse ya mipingo imeneyo.

<sup>3</sup> Ndipo tsopano, Lamlungu mmawa, Ambuye akalola, ife tikuyembekezera nthawi yopambana, chifukwa Lamlungu mmawa pokhala lopuma lathu, kukhala ngati kupumula kuyambira Loweruka usiku... ndi M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Koma Lamlungu mmawa ine ndikufuna ndidzatenge: *Namwali Wopusa*, ndi *Chiukitsiro*, *Foro... Handiredi ndi Forte-foro Sauzande*, ndi zotsalira zazing'ono zonse zimenezo zimene zikumangiriza uthenga pamodzi wa Lamlungu mmawa. Misonkhano idzayamba pa naini koloko. Nkulondola uko, abusa? Pa naini koloko, Lamlungu mmawa, ife tikufuna kuti tidzatolere zinthu zonse zimenezo monga "Kodi chidzachitike ndi chiyani ndi anamwali opusa, ndipo kodi chidzachitike ndi chiyani ndi anamwali ochenjera? Kodi iwo adzabwereranso liti? Kapena kodi handiredi forte foro sauzande adzawonekera pati?" Ndi zinthu zambiri monga zimenezo Lamlungu mmawa, kudzayetsa kudzazimangiriza izo pamodzi, zomwe izo zikugwirizana bwino lomwe ndi uthenga uwu. Ndiyeno Lamlungu usiku ife tidzatenga mngelo wamkulu womaliza ndi Uthenga wopita ku Laodikaya, Lamlungu usiku, Ambuye akalola.

<sup>4</sup> Ndipo tsopano, ndiye, mawa masana padzakhala msonkhano pano, msonkhano wa tepi. M'bale Gene wangondiiza ine kumene kuti iwo . . . ife tidzayamba thuu koloko mawa masana. Ndipo anthu inu amene mumakonda kubwera kudzamvera mauthenga, kukhala ndi pemphero mozungulira guwa, inu amene mukufunafuna Mzimu Woyera kapena chinachake, nthawi yodabwitsa. Mtchalitchi ndi mwabwino komanso mofunda, mumakhala motsegula, ndipo mokonzedwera aliyense pa nthawi iliyonse amene angafune kubwera kudzapemphera ndi kudzafunafuna Ambuye. Tchalitchi chimakhala chotsegula ndipo chimakhala chikudikirira. Ndipo ndife . . . ife tidzakhala tikukuyembekezerani inu, mudzaziike izo monga choncho, tidzakhala tikukuyembekezerani inu mawa masana.

<sup>5</sup> Kapena nthawi iliyonse yomwe inu mungafune kubwera mu tchalitchi kudzapemphera, bwanji, nthawizonse mumakhala mokonzeka. Ndipo ngati iwo zitakhala kuti zitseko ndi zokhoma kapena chinachake, kungowoloka msewu uko, m'bale wanga, amene amasalira pano. Ine ndikuganiza kuti ndi 411, ine ndikukulupirira momwemo . . . Kapena 811 (ndi choncho . . . ?) 811, basi mongopingasa kuchokera ku tchalitchi pano, 811. Bwanji iye, a . . . mkazi wake amakhala ndi kiyi ngati atakokera chitseko pamodzi ndipo icho nkukhomeka, koma iwo amachisiya icho chotsegula mwinamwake mmawa, amachitsegula icho. Kapena, ukatha msonkhano, chimatsekedwa usiku, kuti ana asamathamangemo, inu mukudziwa, ndi kumaswa mawindo ndi zina zotero; inu mukudziwa momwe ana amakhaira, makamaka masiku ano. Chotero ife timatseka pa chifukwa chimenecho. Ife timadana nazo ngakhale kuti tizitseka chitseko pa nthawi iliyonse ku tchalitchi. Mwinamwake pamene chinacho chikadzakonzedwa, ife tidzakhala nazo izo potero zidzakhala mosiyana nthawi imeneyo, ndipo ife . . . winawake akhoza kumadzakhalapo nthawi zonse kuti anthu azikhoza kubwera ndi kudzapemphera, ndi kudzafunafuna machiritso, kudzafunafuna Mzimu Woyera.

<sup>6</sup> Inu, amene mulibe Mzimu Woyera mmooyo mwanu, muzibwera kuno, muzidzakhala pano, muzidzangokhala usiku wonse ngati inu mukufuna kutero, kudzangokhala mpaka inu mutalandira Iwo.

<sup>7</sup> Anali ndani yemwe anali kuno kanthawi kapitako amayimba, “Mulungu paliponse pa ine, ndi Mulungu konsekonse”? Ine—ine ndimaganiza kuti Mkwatulo wafika; ine, ndinayang'ana pozungulira pamenepo, ndi kuwona ngati aliyense alipo. Izo zinali zodabwitsa kwenikweni; ine ndikuyamikira zimenezo. Ife tikhoza kumakhala nazo izo pafupifupi nthawi iliyonse. Inde, bwana. Ndizo . . . Ine ndinangolowa mkati, inali nthawi yoti ndimve zimenezo.

<sup>8</sup> Ndipo ine ndaphonya kuimba konse kwabwino mmisonkhano imeneyi chifukwa ine ndimaganiza mwina

kuti... Oh, ine ndimangokhala wotangwanika kwambiri, inu mukudziwa momwe zimakhallira. Anthu—anthu amabwera pa ndege, sitima, ndi... Iwe—iwe sumadziwa nkomwe izo, inu mukuwona, chifukwa izo zimangobwera mwa foni, iwe umayenera kupita kwa iwo, kukakomana nawo iwo ndi kuwapempherera iwo, ndi kulikonseko. Izo zimangopita mosalekeza, ndipo kenako nkuyesetsa kuti uwerenge aponso; izo zimapangitsa izo kukhala vuto ndithu. Koma nthawizonse timakhala okondwa kukumana ndi anthu ndi kuwachtira zomwe ife tingathe chifukwa ndi... ndizo zathu... ife antchito a anthu kwa Ambuye Yesu Khristu kwa anthu Ake mu tsiku lino. Ndipo ife tingakonde titamachita zambiri kuposa momwe ife timachitira, koma ife sitingathe.

<sup>9</sup> Mtumiki anathamangira mmawa uno, kusokonezeka kwa mitsempha, amangosweka basi, munthu wabwino. Ndipo chifukwa chakuti iye anali... iye anangogwiritsa ntchito. Anali... Anayamba kudzuka, ndipo mtsikana wake wamng'ono anali atayima mchipindamo, iye anangoyamba kuzungulira. Iye anali atavala zovala zogonera zofiira; anati chinthu chomaliza chimene iye akukumbukira chinali kadontho kakang'ono kofiira kakuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, monga choncho. Anatuluka panja, mwaona. Ndipo chotero iwo anathamangira naye mmwamba. Chotero ndizo—ndi ntchito yochuluka kwambiri, inu mwaona. Inu—inu mukukumbukira kuti ndinu azimphamvu ndipo ife—ife timafuna... ife timaganiza kuti katundu yenseyo ali pa ife. Koma, inu mukudziwa, Mulungu ali nawo antchito konsekonse akuti azisamalira zina za zimenezo, ndipo kotero ife timangochita mopambana momwe ife tingathere. Koma mtumiki wachisomo akuyesetsa kuti achite zonse zomwe iye angathe mmasiku otsiriza ano kwa Ambuye wake. Ine ndikutsimikiza... Ndipo Ambuye anamuwombola iye pomwepo, iye ali bwino basi, ndipo anamubweretsa iye ndi kudzamuzungulitsa, mwanthawizonse, alibwino bwino, amapita panjira yake, akusangalala.

<sup>10</sup> Ndipo, oh, chinthu chachikulu chinachitika lero. Ine basi sindikufuna kuti ndiyambe pa zinthu izi, koma... Inu mukudziwa, ine ndinamuuza mkazi wanga, ine ndinati, "Tsopano, pakhala winawake akubwera kumtunda uko, ndipo iye akhala mwamuna, wamfupi, wojintcha, wa tsitsi lakuda ndi maso akuda, iye adzawerenga chikwangwani icho ndipo adzayamba ku... koma iwe udzamuitane iye, wawona." Ine ndinati, "Chifukwa Ambuye ali ndi uthenga wa iyeyo." Ndipo ine ndinadzuka ndi kudzatsegula Baibulo, ndipo ine ndinati, "Ine ndiziyika zinthu izi apa kuti iwe uwone kuti ndizo ndendende zomwe Ambuye akufuna kuti iye adzachite."

<sup>11</sup> Zaka eyiti zapitazo, bambo wachi Poland wochokera ku Poland, anauka ku Poland... Pa msonkhano, iye

anabwera pa nsanja ndipo iwo anati...kapena Mzimu Woyera unamuyang'ana iye, unamuza iye, unati, "Inu mwangosokonezeka." Ndizo zomwe...Iye ankaganiza kuti ndanena ndi ine zimenezo, koma unali Mzimu Woyera utanena. Iwo unakhala naye nthawi yonse, ndipo pomaliza pake unamukokera iye kuchokera ku Mzinda wa Kansas kupita mchipindachi usiku wathawu, ndiyeno iye anasokonezeka kwenikweni pamene anadzamva za ubatizo wammadzi uja. Iye anapita ku hotelo yake, ndipo Mzimu Woyera unati, "Dzuka tsopano ndipo upite kumtunda uko." Winawake amafuna kubwera naye iye, koma iye anakana izo chifukwa mmasomphenyawo iye anabwera yekha. Mukuona? Ndipo chotero...ndipo iye, njonda ngati amafuna kuwerenga chikwangwani, anayambapo, anadzatembenukira kumbali, ndipo mkazi wanga anamuyitana iye ndipo ine ndinapita pakhomu, Ine ndinati, "Ndi—ndi iyeyo, muloleni iye abwere."

<sup>12</sup> Iye anati, "Kodi ine ndichite chiyani?" Iye atatha kuwona, iye anati, "Tsopano ine ndaziwona izo."

Ine ndinati, "Ine ndikufuna ndikuwonetseni inu ichi kuti inu mudziwe tsopano, inu mwaona." Ine ndinati, "Ambuye anandiuza ine kuti inu mukubwera." Inu mukhoza kumufunsa iye. Ine ndinati, "Tsopano, Lemba lake ndi ili. Muwerenge izo pomwe apa inu musanapitirire."

<sup>13</sup> Chabwino, iye ali pano kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu tsopano. Chotero...?...Iye akhoza kukhala kuti ali pano tsopano, kwa zonse zomwe ine ndikuzidziwa. Kodi inu muli pano, m'bale? M'bale, m'bale waku Poland. Huh? Eya, kumbuyo uko iye wakhala pa kona, inde. Imirirani... kwezani dzanja lanu mmwamba kuti iwo akhoze kukuwonani inu pamenepo. Chabwino. Kuwona Mzimu Woyera...Izo zimangochitika nthawi zonse. Anthu ambiri amaganiza kuti masomphenya amangobwera pa nsanja. Oh, izo zimakhala zisanayambe. Nanga bwanji zimenezo, M'bale Leo? Basi kulikonse, mwawona. Chabwino, pano ndi malo aang'ono a Izo, pano. Pano ndi pamene zochepe chabe zimachitikira. Kunja uko nkomwe Izo zimachitika usana ndi usiku wonse, inu mwaona. Eya, mufunsi mkazi wanga, ndipo iye...kapena iwo, ndi oyandikana nawo anga kumbuyo uko, M'bale Wapad, ndi iwo onse omwe andizungulira. Oh, mai! Izi ndi zinthu zapang'ono—zinthu zapang'ono pano; ndi zinthu zazikulu zomwe zimachitika kumeneko. Tsopano, ndipo theka sizinafotokozedwe nkomwe. Oh! Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha izi, podziwa kuti Ambuye wathu akubwera posachedwapa ndipo ife tidzakakhala ndi Iye kwanthawizonse pamenepo; osati *kwanthawizonse*, koma kwa *Muyaya*, kwa Muyaya.

<sup>14</sup> Tsopano, Ambuye akalola, ine ndikukhulupirira kuti ndi pa eyitini, Lamlungu, pa sabata. Lamlungu, pa sabata, pa eyitini. Ndinali ndi nkondo yoyipa; Satana anayesera kundipatsa

ine chimfine ichi chomwe chikuyendayenda kuzungulira kuno, Ine ndimangopitirira kumachibwezera icho kwa iye; ndipo iye amandipatsanso ine, ndipo ine nkuchibwezeranso icho kwa iye. Chotero... ndipo chotero ndithudi ndakhala ndikumenya kankhondo kakang'ono. Chotero ife mwinamwake tithana nayo nkhoodoyo sabata yamawa. Ndiyeno, Ambuye akalola, pofika Lamlungu lotsatira, pa eyitini. Ndipo ife tidzayesa kuti tidzabweretse msonkhano wina kuti tidzapempherere anthu odwala chifukwa iwo ali...zinthuzo zikuthandizira ndi kuthandizira ndi zadzidzidzi zowonjeza zenizeni ife tikuyesetsa kuzisamalira mwachangu momwe ife tingathere, ndipo ma ora, maora onse ausiku ndi chirichonse zomwe zimabwera ndi kupita. Chotero pa eyitini ife tidzakhala ndi msonkhano wanthawizonse wamachiritso. Ndipo ngati inu muli nawo ena a okonedwa anu omwe akufuna kuti adzapemphereredwe, chabwino, inu mudzawabweretse iwo, kapena mudzawabweretse iwo muno pa nthawi imeneyo.

<sup>15</sup> Tsopano, pali anthu ambiri aku Jeffersonville amandiuzza ine, anati iwo amabwera mu nthawi yake kuti adzakhale muno, pafupifupi faivi koloko, anati sipamakhalanso nkomwe malo a magalimoto awo (kapena sikisi). Chotero iwo...ine ndinati, "Chabwino, inu...Awa ndi abale athu odzatichezera kuchokera kulikonse, anthu, azitumiki ambiri." Ine ndinati, "Iwo ali—iwo akukhazikika pa kuphunzitsa kwa Izi."

<sup>16</sup> Ndipo ife tikungoyesera kugunda mfundo zikuluzikulu. Ndipo kenako mtsogolo pang'ono, bwanji, ife tidzakhala nazo izo mu bukhu kuti inu mukhoza kudzaliwerenga ilo ndipo—ndipo ilo lidzakhala pang'ono—tidzakhala ndi zina zowonjezera pang'ono kwa ilo, chifukwa usiku... Inu mukuzindikira, mausiku angapo apitawa, ine ndakhala ndikuyesetsa, ndimatero, ndimasungira mawu, inu mwaona, chifukwa chimake chachikulu chija, ndi chimene ine ndikufuna kuchiwona; pamenepo pamene vumbulutso la Khristu lidzapangidwe mu m'badwo uno, mwawona, za chimene icho chiri.

<sup>17</sup> Ndipo tsopano, ife tisanayambe kuwerenga Malemba... Ndipo ine ndikudziwa kuti mawa ndi tsiku lalikulu lazamalonda pamene ife tonse tidzayenera kuti tidzapite kukagula zofunikira zathu zapanyumba za Loweruka usiku. Ndipo ife tikuyenera kuti tikagule izo Loweruka madzulo kapena Loweruka mmawa, limodzi, kuchitira kuti tidzakhale ndi usiku wa Loweruka wopanda zochitika kuti tidzabwere ku tchalitchi. Kotero ife tiyesera kuti tituluke molawirira usikuuno kuti inu musakhale wotopa kwambiri mawa kuti mukatenge izo, ndiyeno nkudzabwerera ku msonkhano wa masana ndi abale kuno ndi matepi ndi—ndipo komanso mawa usiku.

Tsopano, kodi tingangoyima kwa mphindi kuti tipemphere, ngati inu mungathe.

<sup>18</sup> Ine ndikudabwa, ife tisanapemphere, ngati alipo aliyense pano amene ali ndi zopempha zapadera za pemphero, ngati inu mungalole kuti izo zidziwike ndi dzanja lokwezedwa. Mulungu amawona. Tsopano mukuwona ngati ife tiri mdziko losowa kapena ayi, abale. Ine ndikuganiza nainte-faivi kapena nainte-eyiti pa handiredi a omvetsera anakweza manja awo pamenepo... Tsopano, kumbukirani, inu simungasunthe nkomwe popanda Mulungu kudziwa izo. Mukuona? Iye anadziwa zolinga zanu, Iye anadziwa zomwe inu mukuzipempha.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu:

<sup>19</sup> Atate Achisomo Akumwamba, ife tikuyandikira Chiyero Chanu usikuuno, Mpando Wanu wachifumu, kudzera mu lonjezo Lanu lomwe Inu munanena kuti Inu mudzatimva. Ndipo ngati ife tingakhulupirire, Inu mudzatipatsa ife zomwe ife tazipempha. Ndipo ife tikuvomereza zolakwa zathu zonse. Ife tikuzindikira, Ambuye, kuti ife sitiri—ife sitiri oyenera aliwonse a madalitso Anu. Ife ndife—ife ndife osayenera. Ife ndife palimodzi osayenera, ndipo ife sitikubwera ngati kuti ife tinali—ife tinali oyenera ndipo—ndipo kuti ife tingachite chinachake chachikulu. O Atate, pamene ife tiyang'ana pa Kalvare, izo zimachotsa ukulu wonse kuchoka pa ife, ife—ife sitimadziwa china chirichonse pamenepo koma Khristu ndi Iye wopachikidwayo. Ndiye pamene ife tiwona kuti Iye anauka pa tsiku lachitatu molingana ndi Malemba, kwa kulungamitsidwa kwathu, anabwereranso masiku forte pambuyo pake mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, kuti adzakhale ndi ife mpaka kuwonekera Kwake kowoneka mlengalenga pa nthawi yotsiriza. Ndipo ife tikuwona kuti nthawi yotsiriza ikuyandikira mwachangu kwenikweni tsopano. Ndipo ndife anthu osangalala kwambiri, Ambuye, chifukwa chakuti—chakuti Inu mwatipatsa ife mwayi waukulu uwu.

<sup>20</sup> Ndine wothokoza kwambiri, Atate, kuti anthu omvetsera awa akukhala ndi mitima yoweramitsa, ndikumamvetsera...?.. Ndiyeno, Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu muyeretse milomo yanga usikuuno, ndipo usiku uliwonse ndi nthawi iliyonse yomwe ine ndidzabwere pa guwa Lanu kudzayankhula ndi anthu Anu; chifukwa, Ambuye, musadzandirole ine kuti ndidzayankhule chirichonse cholakwika. Inu mukanali nayobe mphamvu yotseka pakamwa monga Inu munachitira mu dzenje la mikango ndi Daniele. Ndipo ngati ine ndinganene chirichonse chomwe sichinali mogwirizana ndi chifuniro Chanu, mudzatseke pakamwa panga, Ambuye, kuti ine ndisachiyankhule icho. Mulambalale maganizo anga; muniyike ine pa njira yoyenera, Ambuye, pamene sindidzayankhula chirichonse koma Chowonadi. Pakuti ine ndikuzindikira kuti mu tsiku lalikululu limenelo anthu awa adzakhala akudikirira kumeneko pa...

kudikirira molingana ndi utumiki umene ine ndawalalikirira iwo. Ngati Inu mubwera ku—kudzatenga iliyonse ya nyenyezi Zanu, ndi angelo Anu, azitumiki Anu, antchito Anu, iwo adzayenera kuti adzaphunthidwe poyamba molingana ndi Mauthenga awa amene takhala tikulalikirira pano. Inu mudzafuna kuti iwo adzayankhire, antchito Anu.

<sup>21</sup> Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mulole Mzimu Woyera uyankhule ndipo osati munthu. Muvinire mitima yathu kuti ife tikhoze kumumva Iye. Ine ndikhala ndikumvetsera, Atate. Ndikupemphera kuti Inu muchiritse odwala ndi osautsika. Zonse zomwe anthu akuzisowa, kulikonse, mulole chisomo Chanu ndi chifundo zikhale ndi iwo. Mupereke chopempha chirichonse chimene chadziwitsidwa usikuuno pokweza dzanja. Kunja kudutsa mdziko lonseli pamene ena ambiri akuvutika, ngakhale iwo amene akuimiridwa ndi mipango iyi, ndipo zopempha izi zimene ziri pansu pa dzanja langa apa, mulole Mzimu Woyera uyankhe, Atate, ndipo muchiritse odwala. Yankhulani ndi ife tsopano kudzera mu Mawu Anu olembedwa, mwa Mzimu Woyera, ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen. Khalani pansu.

<sup>22</sup> Tsopano, usikuuno mwatentha pang'ono mtchalitchi. M'badwo waukulu wa Mpingo wa Laodikaya ukubwera. Ndipo usikuuno ife tikuyandikirira ku m'badwo wina wawukulu wa mpingo umene uti ukhale—m'badwo wa mpingo wachisanu. Ife tinatenga m'badwo woyamba wa mpingo, umene uli Efeso. Ine ndikhoza kuwerenganso izi kachiwiri pachiyambi, izo zonse zinalembedwa ndipo chotero ine ndikufuna kuti ndikuwerengereninsu inu kwa inu amene mungafune kulwona pamapepala anu.

<sup>23</sup> M'badwo wa mpingo woyamba unali M'badwo wa Mpingo wa Aefeso, kuyambira A.D. 55 mpaka 170. Paulo anali nyenyezi yake, ndipo iwo unali m'badwo wa mpingo woyamba. “Ntchito zopanda chikondi” ndiro linali dandaulo la Mulungu. Mphoto yake inali “Mtengo wa Moyo.”

<sup>24</sup> M'badwo wachiwiri wa mpingo unali 170 mpaka 312, Ireniasi anali mthenga wa tsikulo. Ndipo dandaulo linali kuzu-... linali masautso, ndi mpingo wozunzidwa. Mphoto, “Korona wa Moyo.”

<sup>25</sup> M'badwo wa mpingo wachitatu unali Pergamo, Marteni Woyera anali mthenga wa mpingo umenewo. M'badwo wa mpingowo unali kuyambira 312 mpaka 606. Dandaulo linali “chiphunzitso chabodza, kunama kwa Satana, maziko a ulamuliro wa Upapa, ndipo chikwati chinali mpingo ndi boma pamodzi.” Mphoto inali “mana obisika, ndi mwala woyera.”

<sup>26</sup> Ndipo m'badwo wa mpingo wachinai unali Tiyatira; Columba anali mngelo wa m'badwo wa mpingo umenewo, mthenga; 606 mpaka 1520. Ndipo m'badwo wa mpingo unali

kudolola kwa Upapa, Mibadwo ya Mdima. (Unali usiku wotsiriza, inu mukudziwa, Mibadwo ya Mdima.) Ndipo mpho—mphotho, inali “mphamvu yolamulira mafuko, ndi Nyenyezi Yammawa,” kwa mngelo.

<sup>27</sup> Tsopano, usikuuno, ife tikuyambira pa m’badwo wa mpingo wachisanu, umene uli m’badwo wa mpingo wa Sarde, S-a-r-d-e, Sarde. Ndipo wa mthenga ku m’badwo wa mpingo uwu anali Martin Luther, akukhala wodziwika kwambiri kwa wophunzira Baibulo kapena mphunzitsi uyu, kapena munthu wamba, kani, lero. Ndipo m’badwo wa mpingo umenewo unayamba mu 1520 ndipo unadzatha mu 1750, 1520 mpaka 1750; ndipo m’badwo umene ife timawutcha “M’badwo Wokonzanso.” Ndipo dandaulo linali “Kugwiritsa ntchito dzina lawo lomwe.” Ndipo mphotho ya wotsalira wapang’ono amene anatsalira, inali “Kuyenda pamaso pa Iye mu zovala zoyera, ndipo maina awo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.” Ambuye atidalitse ife pamene tikugwira ntchito tsopano.

<sup>28</sup> Tsopano ife tikuyambira pa ndime ya 1 ya mutu wa 3, ya m’badwo wa mpingo uwu. Uthenga wa ku Sarde, nthawi ya kukonzanso. Wotsalira wapang’ono wokhulupirira anatsalira, basi pafupifupi kutheratu.

<sup>29</sup> Tsopano kwa ena mwa obwerakumene, ndikhoza kunena pa izi apa, kuti...kuti inu musatsalire mmbuyo mu izo. Ndi zakhambi kani, ndipo nthawizina ife tifika pamene ife tidzakhoze kuyika mauthenga athu pa...kuzijambula izo, nkubwera masana ndipo nkudzazikonza izo; ndikhoza kudzachita izo Lamlungu. Tsopano, izi chirichonse chikuyimira woya...m’badwo wa mpingo: wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni. *Ichi* kuyambira ndi Filadefiya...

<sup>30</sup> Ndipo *ichi* apa chikuimira—mphamvu ya Chipentekoste, kapena mpingo umene unali pa Pentekoste. Iwo unali mpingo waukulu ndithu pachiyambi, koma iwo anayamba a—a... Mzimu wachipembedzo ukubwera pakati pawo, ukuyesera kuwupanga chipembedzo Mpingo, zomwe zinkatchedwa “Ntchito za Chinikolai.” Kodi mukukhoza kundimva ine kumbuyo uko? Eya? Chabwino. “Ntchito za Chinikolai.” Tsopano, icho sichinali *chiphunzitso* apobe. Ndiyeno ife tinatenga Mawu ndi kuwaswera iwo pansu, zomwe zinali “ntchito,” zomwe zinali “Chinikolai.” Ilo ndi dzina lachirendo kwa ife, Chinikolai, chotero ine ndinatenga Chigriki ndipo ndinachiswa icho. Ndipo *nikao* amatanthauza “kugonjetsa, kapena kulakika, kapena kulanda chinachake.” Chinikolai, *lai* ndi “mpingo, anthu wamba.” Chinikolai, a—ntchito zomwe zinkayesera kuwalanda anthu wamba, ndi kukayika madalitso onse, ndipo mmodzi yekhayo amene angawerenge Baibulo, mmodzi yekhayo amene angapereke kutanthauzira, ayenera kukhala bishopu, kapena munthu wina wamkulu wa mpingo.



<sup>31</sup> Ndiye ife tikupeza kuti, mu m'badwo wa mpingo wachiwiri, iwo ukanayamba kufinyikira kunjja. *Ichi* chikadali Pentekoste; ndipo *ichi* ndi chipembedzo (d).

<sup>32</sup> Tsopano, mu m'badwo wa mpingo wachitatu, Pergamo, Pentekoste anali pafupifupi atafinyidwira kunjja. Koma chiphunzitso cha chipembedzo, icho chinadzasandulika kuchokera ku “ntchito” *apa*, njira yonse mpaka ku “chiphunzitso” *apa*. Pamenepo iwo anali atalowadi kwenikweni, anakwatirana pomwe *apa*. Iwo anakwatirana! A. . . gulu ili *apa* lomwe linali litagonjetsa magulu achipentekoste.

<sup>33</sup> Tsopano momwe ine ndikunenera izi, abale, zimenezo ndi zoonazzeneni. Zimenezo ndi mogwirizana ndi zolembedwa zopatulika za mbiriyakale. Ma bukhu a Nicene Council, *Foxe's Book of the Martyrs*, ndi zolemba zonse zazikulu za amakedzana. Ine ndiri nazo zina za zolembedwa zakale kwambiri zomwe ziripo. Ndipo mmodzi aliyense. . . Ine ndikunena izi osati ndi. . . Sindikunena kuti ndine wa Pentekoste. Izo sizikutanthauza kuti. . . Pamene ine ndikuti “pentekoste,” izo sizikutanthauza bungwe ili la tsiku lino limene ife tikukhalamo. Amenewo ndi olakwa basi monga ena onsewo. Koma ine ndikutanthauza chipentekoste chenicheni, Mzimu weniweni wa Mulungu ndi Chiphunzitso chapachiyambi, ndi madalitso apachiyambi, ndi mayina apachiyambi, ndi chirichonse ndendende momwe izo zinayambira pachiyambi monga momwe zinkayendera mu Baibulo.

<sup>34</sup> Tsopano, ndiye pamene ife tikubwera ku m'badwo *wuu*, inu mukuwona utali womwe Pentekoste wafikako. Kodi inu mukutha kuwona izo kumbuyoko bwino? Kodi inu mukutha kuzimvetsa izo kumbuyoko? Chabwino. Tsopano, apa pakubwera, usiku watha, m'badwo waukulu umene ife tirimo *apa*, Konstantini, Konstantini, *K-o-n-s*; ine ndilemba izo. Iye, pokhala wachikunja, anali. . . anawafunsa Akhristu awa *apa* (omwe anali ndi chiphunzitso cha Chinikolai) ngati iwo angapemphere kuti iye akapambane nkondo inayake; chabwino, iye akanadzakhala Mkristu. Panthawi imeneyo pamene iye anali kunkhondo, iye analota loto kuti iye ayenera. . . Ndi mtanda woyera umene unayikidwa patsogolo pake, iye anati, “Ndi ichi iwe ukapambana.” Ndipo uko nkulondola. Kenako iye anadzutsa gulu lake lankhondo ndipo anajambula pa zishango zawo mtanda woyera, ndipo amenewo anali malo obadwira kapena chiyambi cha dongosolo la Chikatolika, lero, lotchedwa Knights of Columbus.

<sup>35</sup> Tsopano—tsopano, Konstantini, pali. . . inu simungakunkhe chinthu chimodzi ku mbirizakale, za iye kukhala wotembenuka. Iye sanali kanthu koma tambwali wandale. Iye anali nalo m'malingaliro mwake ganizo lakuti—lakuti agwirizanitse ufumu wake ndikuwupanga iwo kukhala wamphamvu. Chotero iye mwa iyemwini, pokhala wachikunja, ankapembedza mafano;

kenako iye anawona kuti chiphunzitso cha Chinikolai chinali pafupifupi chitafinyidwiratu mpaka kufika pamalo, chotero iye anagwiritsa ntchito njira yomweyo imene ife tinaipeza usiku wathawu.

<sup>36</sup> Ndipo Yesu ananeneratu izo zaka firii handiredi ndi foro izo zisanafike pochitika, kuti iye akanadzaphunzitsa chiphunzitso cha Balaamu. Momwe kuti Balaamu anawanyenga ana a Israeli, anawapangitsa iwo kuchita ziwerewere ndipo—ndipo anapereka... anatenga zinthu zoperekedwa ku mafano, kudya zinthu. Tsopano, ife tikudziwa kuti “kudya zinthu izi zoperekedwa ku mafano,” chomwe izo zinali kwenikweni, kunali kupembenda. Akalowamo, iwo ankagwadira mafano, anabwezeretsanso mafano mu mpingo wa Chikristu; chimodzimidzi monga momwe Balaamu ankachitira kumbuyo uko, anapangitsa Israeli kuti achite ziwerewere, kuti apite ku phwando lalikulu ili la fano.

<sup>37</sup> Chabwino, Konstantini anachita chinthu chomwe chomwecho ndi kachitidwe kake, ndipo iye anapanga mpingo. Iye anapereka zochuluka ku Nicene Council, ndipo kenako iwo... Iye anapanga a—nyumba zazikulu zochuluka zimene iye anali nazo, ndipo iye anazisandutsa izi kukhala matchalitchi. Ndipo kenako iye anapanga guwa lalikulu la nsangalabwi lansembe, lokongoletsedwa ndi golide ndi miyala yamtengo wapatali. Pamwamba pakepo iye anaikapo ngati mpando wachifumu, ndipo iye anampanga munthu mmodzi mtsogoleri ngati... iye ankatchedwa pamenepo “bishopu.” Ndipo anakamuyikapo iye pampando wachifumu umenewu, Boniface III analongedwa ufumu. Sikuti iye amangoyenda kokha atavala zovala monga wo—wosauka ankachitira, koma iwo anampangira iye mwi—mwinjiro wabwino kwambiri ndipo anamuveka iye ngati mulungu ndipo anadzamukhazika iye pamenepo ndipo anamutcha iye “Vicar.” Vicar, kapena *Vicarius Filii Dei*, izo zimatanthauza “mmalo mwa Mwana wa Mulungu.”

<sup>38</sup> Tsopano, izi ziri kwa iye amene ali ndi nzeru, jambulani, lembani zimenezo: *Vicarius Filii Dei*. Ndiyeno inu mukajambula mzere pansu apa ndi kuwonkhetsa manambalawo, ndipo inu mupeza ndendende chimene Mulungu anati chilemba cha chirombo chinali: sikisi handiredi ndi sikiste-sikisi. Mukuona, *Vicarius Filii Dei*... Tsopano, ine ndinafikako ku Roma ndipo ndinafikako ku Vatican. Ndipo korona wa patatu: ulamuliro wa gehena, kumwamba, ndi purigatorio. Mukuona? Ndinayiwona nduwirayo, ndinawona chovala, ndinawona zonse, pomwe apo.

<sup>39</sup> Kwenikweni, Lachinayi masana pa firii koloko ine ndimayenera kukumana ndi papa *womaliza* yemwe anali kumeneko. Baron von Blomberg anali ndi... ndipo kenako iye anati, “Tsopano, pamene inu mukupita, M’bale Branham, chinthu choyamba chimene inu muyenera kukachita ndi

kugwada pa bondo lanu lakumanja ndi kukapsyopsyona mphete imeneyo.”

40 Ine ndinati, “Izo ndiye ayi. Izo ndiye ayi. Mungoiwala zimenezo.” Ine ndinati, “Ine ndimapereka. . . Ine ndiribe kanthu kotsutsana naye munthuyo, iye. . . ? . . .” Koma ine ndinati, “Pali chinthu chimodzi, ine ndimpatsa munthuyo udindo wake. Ngati iye ali ‘M’busa,’ izo ndi zabwino, ‘Bishop, Eledara, Dotolo,’ chirichonse, ine ndidzapereka ulemu kwa munthuyo mokondwera. Koma kumupembedza munthu? Ine ndimapereka ulemu wanga kwa Munthu mmodzi: Yesu Khristu. Ndiye Munthu yekhayo yemwe ine ndinganamugwadire.” Ine ndinati, “Ingoiwalani zimenezo. Ingochotsanipo zimenezo.” Ine sindingachite zimenezo. Ndipo kotero ine. . .

41 Nditabwerera kunyumba ine ndinapeza kuti kunali wachi Amerika wina wamkulu yemwe anachita zimenezo, nayenso, Teddy Roosevelt. Iye anakana kuchita zimenezo chifukwa cha. . . Mukukumbukira zimenezo mu mbiriyakale? Kuti iye anakana kuti amuwone Papa chifukwa iye amayenera kuti amupsyopsyone mphete yake kapena. . . Iwo anali atavala iyo pa chala chachikulu, aponso, inu mukudziwa. Chotero. . . Oh, ayi. Ayi, izo ndiye ayi. Chotero ndiye. . .

42 Komabe, mu. . . Tsopano, monga Balaamu. . . Ndiye ife tinapeza usiku watha, uko. . . Tsopano, apa poyamba, ife tisanachoke apa, iwo anawupanga chitaganya mpingo ndipo anakwatira, anatenga malingaliro ena achikunja, mafano achikunja omwe anali mu mpingo. Mulungu wa Jupiter, mulungu wa dzuwa, mulungu wa Mars, mulungu wa Venus, ndi mafano onse awo a milungu ndipo iye anaichotsa yonseyo kuichotsa mu mipingo yachikunja; ndipo anakaikamo Paulo, Petro, namwali Maria, onse amenewo, ndipo anati, “Vicar wanu ndi uyu chifukwa Yesu anamuza Petro, ‘Ine ndikukupatsa iwe mafungulo,’ ndipo iye ndi wolowa m’malo wautumwi.” Chimenecho chikadali chiphunzitsa cha Chikatolika mpaka lero. Ndipo iwo anaikamo mafano. Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Anabweretsa kupembedza mafano mu Chikhristu, chotchedwa Chikhristu; osati Chikhristu chenicheni, chifukwa achipentekoste apang’ono. . .

43 Tsopano kumbukirani, ine sindikuti. . . Ine sindinati, “Abaptisti, Amethodisti, Apresbateria,” iwo ali mkati onsewo. Koma chenicheni, chipangizo chenicheni cha Mulungu chinali pentekoste; chinali, ndi, ndipo chidzakhala chimenecho nthawizonse! Ndi kumene Mpingo unayambira, pomwe apa ndi Mphamvu ya Chipentekoste.

44 Tsopano, inu mukuti, “Nkulondola uko, M’bale Branham?” Ine ndikufunsani inu kuti mutenge mbirizakale, ndipo muyang’ane pansu kudutsa mzere wa nthawi mpaka pano, ndipo mupeze ngati mmodzi aliyense wa enieniwo, ana owona

a Mulungu sanagwiritsitse ku Madalitso Achipentekoste amenewo; anayankhula mmalirime, anatanthauzira malirime, amakhala ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, amabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Chirichonse chimene atumwi ankachita, iwo ankachita nawonso, kumatsika kudutsa monse mmenemo. Ndi chifukwa chake mmenemo, powerenga mbiriyakale, ine ndinatenga Paul ndi Ireniasi ndi—ndi—ndi—ndipo mpaka kwa Martin Woyera, Columba; aliyense wa amuna amenewo (kumatsika mpaka mu m'badwo uno kuno), anali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa.

<sup>45</sup> Chabwino. Iye anati iwo anali. . . choyankhulira chinali ndi pang'ono. . . Kodi ziribwino pamenepo? Chabwino. Ayi, iwo akupukusa mutu wawo, iwo sakukhoza kumva nkomwe tsopano, Billy. Chabwino. Kodi mukutha. . .? Kodi ziku. . .? Tsopano, inu mukundimva ine tsopano? Tsopano, bwanji pamenepo? Kodi ziriko bwino? Eya? Aliyense akuti, “Chabwino.” Paul, iwe walephera marikisi amodzi. Chabwino, zabwino.

<sup>46</sup> Tsopano, mu m'badwo uwu apa ndiye pamene iye anapanga chinthu chachikulu ichi, ndipo nkudzamuika munthu uyu apa ngati bishopu wapadziko lonse pa mipingo yonse, nkuwapatsa iwo ndalama zochuluka ndi zina zotero, ndipo kuwalonjeza iwo, ndipo nkulumikizitsa mpingo ndi dziko pamodzi, ndi kuwulola mpingo uzilamulira boma. Anamupanga iye kukhala munthu wopambana. Chotero apo pali ndendende. . . Zimene Konstantini anachita ndi chinthu chomwe chomwecho chimene ife tinachipeza uko mu mpingo wina uwu, kuti nzomwe Mulungu ananena; kuti, mmasiku a Eliya, kuti iwo anamulola mkazi uja Yezebeli kuti agonjetse ana Ake; izo zinachitika mu M'badwo wa Mdimba. Ndipo tayang'anani apa pamene Pentekoste ili tsopano. Mai, mai! Anangoipangitsa mdimba iyo. Ndipo kwa pafupifupi zaka wani sauzande, izo. . . kuyambira pafupifupi 500 mpaka 1500, kulondola, ndiwo 606 mpaka mma '530. . . '520, ndi manambala enieni, koma pa zaka wani sauzande. Iwo adzatero. . . kuzunza kwa magazi. Mukawerenge mbiriyakale.

<sup>47</sup> Tsopano, Mkatolika adzakuuzani inu kuti mpingo wa Chikhristu, iwo anali mpingo wa Chikhristu. Iwo ndi mpingo *wachipembedzo* cha Chikhristu. Koma achipentekoste owona ankatulutsidwa panja, nkukaphedwa, ndipo anaphedwa, ndi kuphedwa ndi mapapa ndi mabishopu ndi ena otero, mwamagazi momwe izo zikanakhilira.

<sup>48</sup> Tsopano, tsikulina izo zidzanditengera ine moyo wanga, mwaona, kunena zimenezo. Koma ndicho chinthu chimodzi chotsimikizika, ine ndikudziwa njira yomwe ndikulowerako, tsopano ine ndikudziwa. Zikungowukhabe magazi. Koma oralo likufika tsopano, lomwe inu mukuwona mogwirizana ndi zomwe zikuchitika mu fuko kuti sipatenga nthawi yaitali. Inu musati mubwerere konse kuchoka pa Icho! Icho ndi Choonadi. Khalani

molondola ndi Icho. Musakanize magari anu monga iwo a mu tsiku limenelo.

<sup>49</sup> Tsopano, apa inu mukuona zomwe zinachitika. Ndiye apa chiphunzitso cha Yezebeli chinadzalowamo. Yezebeli anali mkazi, wachikunja yemwe. . . Ahabu anachita chinthu chomwe chomwecho chimene Konstantini anachita; anakwatira mkazi uyu pofuna kuti alimbikitse ufumu wake, ndipo anabweretsamo kupembedza mafano mu Israeli ndendende basi monga momwe Konstantini anachitira kumbuyo uko. Ndipo Pentekoste inali pafupifupi itatheratu kwathunthu.

<sup>50</sup> Tsopano, Mulungu anamuukitsa Martin Luther. Ine ndikufuna kuti inu muzidikire momwe izo zimachitikira *apa* ndipo pafupifupi kuzimiriratu kwathunthu, ndiye mosayembekezera zinayambira *apa*, ndi kumatsikira mmusi *apa* kachiwiri. Ndipo ine ndinakhala ngati ndinalamba izo pamene chifukwa ndi—ndi phunziro lalikulu la Lamlungu usiku, Ambuye akalola.

<sup>51</sup> Tsopano—tsopano, ine ndikukhulupirira ife takhala ngati takodwapo kale tsopano pamene ife tiri. Tsopano, pomwe apa *umu* ndi—M'badwo wa Mdimu, pomwe apa, kuyambira 1500 . . . kuyambira 606 mpaka 1520. Momwemu umu. Ine ndiziika izi apa kuti inu mudza . . . 606 mpaka 1520. Umenewo ndiwo M'badwo wa Mdimu, mpingo uwu pomwepa *apa*, M'badwo wa Mdimu. Tsopano, mpingo uwu umene ife tikufikamo tsopano ndi mpingo wa Luther.

<sup>52</sup> Tsopano, pafupifupi aliyense kumbuyo uko, anthu amenewo anafera mu. . . Amuna awa monga Ireneyasi, ndi Martin, ndi Columba, ndipo iwo anazimirira. Ndipo tsopano mumutenge aliyense amene akufuna kufufuza mbiriyakale iliyonse imene inu mukufuna, ngati iyo ili mbiriyakale yovomerezeka, ndipo pamene iwo akuuzani inu kuti “Patrick Woyera anali Mkatolika,” iwo sakudziwa zomwe iwo akunena. Patrick Woyera anatsutsa mpingo wa Katolika, ndipo sanapite konse ku Roma, ndipo anakana molimba chiphunzitso chawo. Ndiko kulondola ndendende. Inu mupite kumpoto kwa Eng- . . . kapena Ireland lero, ndipo inu mukawonako chinthu chomwecho. Patrick Woyera anali munthu wa Mulungu! Koma, Patrick Woyera, pamene izo zinanena mmenemo kuti iye—iye anathamangitsa njoka zonse kuzitulutsa mu Ireland, zimenezo zinali nthano.

<sup>53</sup> Ndi angati a inu amene munawerengapo ndi kumvapo za William Tell akuwombera apulo pamutu pa mwana wake? Imeneyo ndi nthano ya Katolika, panalibepo mawu okudza izo. Ine ndinakafikako kumeneko kumene ankaganizira kuti zinachitikako. Izo zinalembedwa pamene, “nthano, si choncho,” mu Switzerland. Billy ndi ine tinali titakhala pamene pambali pa Nyanja ya Lucerne komwe iye anachita chi—chinthucho chinali, iye anawombera munthu; izo nzoona,

koma osati apulo pamutu pa mwana wake. Izo ndi nthano chabe, tizikhulupiro ndi zinthu, izo sizinali nkomwe chomwecho. Iwo alibe zolembedwa za zimenezo kumeneko, kumene izo zinachitikira kapena chirichonse, kuti iwo anayamba achitapo izo. Ndipo izo kwenikweni zikumulavulira iye panja pamenepo ndi kunena zomwe izo zinali. Tsopano, koma mu izi, si kwenikweni mbiriyakale imene imanena kuti iye anachita zimenezo. Mwaona.

<sup>54</sup> Chotero tsopano umu apa, mu m'badwo wa mpingo, ndi pamene izo zinadzazilara, kupitiratu kwathunthu osakhalaponso. Tsopano mu m'badwo wina uwu mukubwera m'badwo wa Kukonzanso. Tsopano, zinthu izi kuno zitatha pafupifupi zaka masauzande zakuda ndi mdima ndi kuzimirira, ndi zina zotero monga choncho, mpingo unakhala ngati unataya kupenya kwa Ireniasi. Iye anali munthu wopambana, munthu waumulungu. Momwemonso anali mahandiredi ambiri a oyera ofunikira amenewo omwe anapereka magazi a moyo wawo mwaulere (ataima mu bwalo limenero) momwe iwo akanathera, mwaona, chifukwa cha Khristu, chifukwa cha ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa choyankhula mmalirime, chiukitsiro cha Yesu Khristu chikukhala moyo mmoyo ndi kukhalapo Kwake Kwaumulungu kumeneko, pamene anthu omwe *amadzitcha* okha Akhristu ankawazunza iwo. Ndiko kulondola. Ndizo ndendende.

<sup>55</sup> Oh, ndi—ndi gulu la ziwanda loyenera gehena ine sindikudziwa chiyani. Anabwera monga choncho ndipo anadzazisonkhanira okha ndi kudzipangira okha, “amadzitcha yekha mneneri wamkazi, wotanthauzira Wauzimu wa Mawu, palibe aliyense amene amadziwa zimenezo koma iwo.” Amadzitcha yekha, koma iye ndi wabodza. Inu mukuona? Ndizimenezotu mwaona. Koma mu nthawi yomweyo; anamutengera mngelo Wake kumeneko, ndi Choonadi. Choonadi nthawizonse chidzabwerera kwa Ichi. Mukuona? Nthawizonse chimabwerera ku chapachiyambi, chifukwa Mulungu samasintha kuchoka kwa Icho.

<sup>56</sup> Tsopano, ndipo ife tinapezanso kuti, usiku watha, ife tisanasiye izi, kuti izo zikhazikike mu mtima mwanu. Sikuti zinangotero . . . Mwa choyimira, Yezebeli, iye anali ndi—mwana wamkazi. Inu mukukumbukira zimenezo? Ndipo Chivumbulutso 13 anati mpingo wachinyengo uwu, Roma, unali ndi ana aakazi. “Iye anali mayi wa timahule.” Nzoona zimenezo? Yezebeli anali ndi mwana wamkazi, ndipo kodi Yezebeli anachita chiyani ndi mwana wake wamkazi? Onani momwe zinthu zonsezo, zoyimira ndi mithunzi. Yezebeli anawonetsetsa kuti mwana wake wamkazi akwatiwe ndi Yehoram, yemwe anali mwana wa Yehosafati mu Yudeya.

<sup>57</sup> Israeli anali atagawanika pa nthawiyo, monga chonchi. Apa pali Yerusalemu *apa*, ndipo apa pali Yudeya *apa*. Chabwino,

Ahabu anali *apa*, ndipo Yehoramu anali *apa*. Chabwino, Yezebeli anali atagonjetsa *izi*, Israeli yense anatenga mafano. Ndiye. . . (Onse kupatula Eliya ndi kagulu kakang'ono kokhulupirika kaja.) Chabwino. Tsopano, kumbali ina *iyi* Yehoramu amayang'anira Yuda; ndipo pamene iye anali ndi mwana mwa Ahabu, iye anamutenga mtsikana uyu ndipo anakamukwatitsa iye kwa mwana wamwamuna wa Yehoramu. . . kapena kwa mwana wamwamuna wa Yehosafati yemwe anali Yehoramu, ndipo anabweretsa kupembedza mafano mu Yuda, ndipo anayika maguwa achikunja mu Yerusalemu.

<sup>58</sup> Ndizo ndendende zomwe mpingo wa Katolika unachita! Iye anaphatikapo chiphunzitso chake cha chipembedzo ndi zina zotero, ndi kuwuchotsa Mzimu Woyera mu mpingo kumusi *kuno* ndi mwana wake wamkazi (Achilutera, Amethodisti, Abaptisti, Apentekoste, ndi ena otero). Ndizo ndendende zimene iye anachita. Baibulo linati, "Iye ndi mayi wa timahule."

<sup>59</sup> Tsopano, inu mungoyang'ana kudutsa m'Malemba. Inu mukawona—inu mukawona china chosiyana motsemphana mu Lemba, ndipo mbiriyakale ikumenya ndendende pa mfundo zomwezo, inu mudzabwere kwa ine ngati njonda. Mukuona? Uko nkulondola. Mulibemo mmenemo!

<sup>60</sup> Zipembedzo izi ndizo zinthu zachiphe zomwe ife tinayamba takhalapo nazo mu Chiprotestanti, kuyesera kuwapanga anthu kuti aziwuyendetsa mpingo, fano lina longa ilo lomwe linadzakhala pa mpandowachifumu umenewo. Bishopu wamkulu, oyang'anira onse a Pentekoste, "Chabwino, tsopano, ndiloleni ine ndiwone, chiphunzitso chake ndi chiyani? Oh, iye amabatiza mu Dzina la Yesu? Iye sangabwere mu izi. Ayi, bwana, abale. Inu mwawakana Iwo." Ndipo izo zakanidwanso nazonso. "Ine ndikumatsani inu kuti mumvetsetse, kuti aliyense wa inu asapite kumsonkhano kumeneko. Chala pansu. Kaya inu mukudwala bwanji, muzitalikire kutali, ziribe kanthu kuti Mulungu akuchita chiyani. Ngati inu simukuyang'ana kudzera mmagalasi athu, bwanji, inu simukuziwona izo nkomwe." Atenga fano la chirombo! Ndipo fanolo linali ndi moyo woti liyankhule. Ndizo ndendende kulondola. Inu simukuganiza kuti iye akhoza kuyankhula, mudzangomuputa iye pang'ono nthawi imodzi. Uh-huh, ndithudi mukhoza kulowa mmavuto.

<sup>61</sup> Ine ndikukumbukira, ku Tulsa, Oklahoma, ine ndinali. . . Oh, ine ndimalowa mu chisokonezo chowopsya kumeneko, zipembedzo zimenezo zinayamba kuzungulira pamenepo. Ndipo ine ndinali nditakhala mchipinda ichi tsiku lina ndipo ndinawona ma—masomphenya. Ine ndinawona ka—kakang'ono. . . kokongola, kamwana ka mphaka kakang'ono, ndipo iko kanali katagona pa pilo ya silika, ndipo iko kanali kanthu kakang'ono kokongola kwambiri. Ndipo ine ndinapita pamenepo (ndipo ine ndimawopa mphaka), ndipo ine ndinapita pamenepo ndipo ine ndinayamba kumususita iye,

ndipo iye amapanga, “puruu, puruu.” Inu mukudziwa momwe iwo amachitira phokoso loseketsa, inu mukudziwa. Ndipo ine ndimamusisita iye, ine ndinati, “Kokongola, kamphaka kakang’ono.” Ndipo iye anati, “puruu,” zabwino basi, inu mukudziwa.

<sup>62</sup> Ndipo ine ndinayang’ana kuseri kwa pilo wake, kunati, “Mphaka wa Chipentekoste.” Chabwino, ine ndinaganiza, “Tsopano, kodi zimenezo sizachirendo.” Ndipo ine ndinati, “Izi ziyenera kukhala masomphenya.”

<sup>63</sup> Ndipo Chinachake chinati, “Bola ngati iwe uzimuisisita ubweya wake mbali iyi, ziri bwino; koma tsopano ngati iwe ukufuna kuwona chomwe iye wapangidwa nacho, uwusisite ubweya wake chammbuyo.” Mukuona? Chotero pamene ine ndinasisita ubweya wake chammbuyo, maso amenewo anatulukira, obiriwira, ndipo iye anali chirombo atayima pamenepo akundilavulira ine molimba mmene iye akanathera. Mwaona, kungosisitira ubweya wake chammbuyo pang’ono pokha. Muuzeni iye ubatizo wake mu “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” ndi wa mdierekezi komanso ndi wa mpingo wa Katolika, muwone zomwe zimachitika kwa iye. Mukuona? Ubweya wake umadzukapo.

<sup>64</sup> Ine ndinabwera uko, ndinati kwa M’bale Gene ndi iwo, kumeneko. . . oh, M’bale Leo ndi iwo, ine ndinati, “Ine ndithudi ndinali ndi masomphenya enieni a zipembedzo za Chipentekoste mu izi.”

<sup>65</sup> Tsopano mutu wa 3, tiyeni poyamba. . . Sarde ndi mpingo wakufa. Ndi wakufa chifukwa iwo anaphedwa panthawi imeneyi. Basi kutambasula pang’ono kwa Moyo, ife tipeza mu mphindi pang’ono zomwe izo zinali, pang’ono pokha. Kuchokera mu 1520 mpaka 1750 unali M’badwo uwu wa Sarde. Ndipo nyenyezi, kapena mngelo wa. . . Nyenyezi yomwe inali mdzanja Lake, yemwe anali mngelo kapena mthenga wa m’badwo wa mpingo umenewo. Kodi zimenezo zikumveka bwino? Kuti nyenyeziyo inali mngelo, ndipo mngelo ndi mthenga wa m’badwo umenewo. Chabwino. Chabwino.

<sup>66</sup> Tsopano ife tatsiriza Nicene Council. Iye anafa kumbuyo uko, ndipo onse anadzabwera mu mphamvu ndi ulemelero, mpingo ndi boma zinadzalumikizana. Ndipo kodi aliyenze angakumbukire zomwe phunziroli linanena usiku watha, zomwe ambiri a anthu amenewo ankaganiza? “Zakachikwi zinali zikuchitika.” Ndipo onse. . . “Kubweretsamo Zakachikwi popanda kubwera kwa Khristu.” Mukuona? Kubwera kwa Khristu kumabweretsa Zakachikwi, chinthu choyambirira. Ndipo mmasiku amenewo iwo anali. . . Ngati inu mungatenge mbiriyakale, inu mudzapeza kuti iwo anali nawo a Yesu abodza amene anadzawukapo ndi china chirichonse, mwaona. Ndipo mpaka iwo ankaganiza kuti papa anali Yesu, kumamutcha



iyе *vicar*, “mmalo mwa Mwana wa Mulungu.” Eya, mulungu wamkulu woyera, chomwecho, atakhala pamenepe.

<sup>67</sup> Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Baibulo limanena kuti pamene Yesu adzabwera...Iye asanafike, “Padzauka aneneri abodza, ndipo padzauka a Yesu abodza.” Uko nkulondola. “Taonani, apa...” Koma ndiroleni ine ndingogwetsera ichi mu mtima mwanu: sipadzakhala konse Yesu atapondetsa phazi pa dziko lapansi lino mpaka Mpingo utakwatulidwa ndipo utapita. Tsopano, inu mungosunga zimenezo mmalingaliro, chifukwa padzakhala akhristu abodza ati adzawukepo. Koma Yesu sadzakhala kuno padziko lapansi; chifukwa lipenga lidzalira, ndipo Iye sadzabwera konse, ife tidzakumana naye Iye mu mlengalenga. Mpingo wapita kale. Ndiyeno pamene Yesu azidzawonekera, uko kudzakhala kubwereranso. Amitundu adzapita kukakumana naye Iye mu mlengalenga. Kodi limenelo ndi Lemba? Mukuona? Iwo adzapita kukakumana ndi Iye mu mlengalenga, ndiyeno ife tidzapita mmwamba. Ndipo Yesu ndi...sadzapondetsa konse phazi Lake pa dziko lapansi mpaka Mpingo utadzakwatulidwa ndi kutengedwera Kunyumba ndipo Phwando la Chikwati likuchitika Kumwamba; kenako Iye adzabwerera kumutsatira wotsalira wa Chiyuda.

<sup>68</sup> Chotero, tsopano, izo zinali zitatha, Nicene Council. Mpingo unali uli—unali uli pansu pa ulamuliro wa upapa pafupifupi zaka sauzande. Iwo anali atapha onse omwe sanagwirizane ndi iwo. Uko nkulondola. Iwe mwina umayenera kubwera pansu pa zimenezo kapena iwe uma—iwe uma—iwe umaphedwa, monga Yezebeli anachitira kwa Israeli.

<sup>69</sup> Mzimu Woyera unali utachokapo palimodzi koma owerengeka okha ochepa mu m'badwo uwu, monga Eliya ndi otsalira a Israeli omwe anali asanagwadire Balaamu. Ngati inu mukufuna kuti muwerenge zimenezo kumusi uko, amenewo ndi Mafumu Woyamba, mutu wa 19, ndi ndime ya 18, pamene Eliya anaima kumbuyo uko m'mphanga ndipo iye anati, “Ambuye, iwo—iwo apha aneneri Anu onse. Iwo achita chirichonse, ndipo ine—ine ndiri ndekha. Ndipo ndine ndekha amene ndapulumuka.” Koma Mulungu anamuuzwa iye Iye anali ndi mahandiredi angapo apobe omwe anali asanagwadire bondo lawo kwa Baala, mwa anthu wamba kunjа kumeneko.

<sup>70</sup> Ndipo chotero, Sarde, tsopano ife tikuyambapo. Mawu omwewo a *Sarde*, ndime ya 1. Mawu akuti *Sarde*, mu mawu a Chingerezi, amatanthauza, ngati inu mukufuna kukayang'ana izo, amatanthauza “uyo wopulumukayo.” *Sarde* weniweni anali “uyo wopulumukayo.” Ndi chimene *Sarde* amatanthauza, chabwino, “uyo wopulumukayo.” Tsopano, mwaona, ndipo “uyo wopulumukayo.”

<sup>71</sup> Tsopano ife tiyambira pa ya 1. Kwambiri... Ife tiwutchula iwo kuti *m'badwo wa Kukonzanso* ndipo ndi chinthu choyenera kwambiri pa kukonzanso uku ngati ife tingachitchule icho chomwecho, chifukwa ndi... Kukonzanso kunali “iwo opulumukawo” amene anachokako ndipo anapulumuka mu zimenezo.

<sup>72</sup> Tsopano tiyeni titenge ndime ya 1:

*...kwa mngelo wa mpingo wa Sarde lemba; Zinthu izi anena iye amene ali nayo... Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri; Ine ndikudziwa ntchito yako, kuti iwe uli ndi dzina lakuti uli ndi moyo, ndipo ndiwe wakufa.*

<sup>73</sup> Tsopano malonje. Tsopano, Mizimu isanu ndi iwiri ili... “Mizimu isanu ndi iwiri ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri.” Mizimuyo inali angelo amene amapita kwa nyenyezi zomwe zinali mithenga. “Mizimu isanu ndi iwiri,” nthawi zisanu ndi ziwiri zosiyana zimene Mzimu Woyera ukanadzazozo mthenga, yemwe anali nyenyezi mu tsiku lake. A—Mzimu ndi Wamuyaya, ndi nyenyezi yomwe inapangidwa ndi cholinga chakuti ikanyezimiritse Kuwalako mu mdima wa mibadwo ya mpingo iyi kumene makandulo ndi nyenyezi zikuyimira. Mngelo, Mzimu, ndi amene amapita kwa nyenyezi ndipo amakanyezimiritsa Kuwala kwa Mzimu Woyera kudzera mwa nyenyezi iyi ku m'badwo wa mpingo umenewo. Kuti, mukhoze kudziwa... ndikudabwa kuti Mizimu isanu ndi iwiriyo ndi ndani. Ndi amithenga asanu ndi awiri a mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Mukuona? Tsopano, ndipo nthawi iliyonse yomwe nyenyezi imabwera powonekera, Mzimu Woyera umatsika ndipo umadzadzazozo nyenyezi imeneyo ndi kuisunga iyo chimodzimodzi basi monga momwe inaliri yoyamba.

<sup>74</sup> Tsopano ndiroleni ine—ndiroleni ine nditsimikizire izo kwa inu. Paulo anati, ngati mukufuna kudziwa kuti inali nyenyezi ya mtundu wanji. Chifukwa, kumbukirani, Satana ndi nyenyezi, nayenso, nyenyezi yammawa. Tsopano zindikirani, Paulo anati... Kodi inu mukukhulupirira kuti iye anali nyenyezi yaku mpingo waku Efeso? Iye anati, tsopano, ngati inu mukufuna kudziwa ngati Izo ziri zoon kapena ayi. Mu Agalatiya 1:8, Paulo anati, akuyankhula pamenepo, kuti nthawi ikanadzabwera, ndipo mimbulu yolusa ndi zina zotero, iye anati, “Ngati mngelo atsika kuchokera kumwamba ndi kudzaphunzitsa uthenga wina uliwonse...” (Tsopano, iye ankadziwa kuti munthu uyu anali kubwera yemwe ankawoneka ngati mngelo ndi *vicar* wamkulu.) Iye anati, “Ziribe kanthu yemwe iye ali, ngati mngelo aliyense kapena winawake abwera ndipo nkudzaphunzitsa chinthu china chirichonse chosiyana ndi Uthenga uwu umene ife takuphunzitsani inu, muloleni iye akhale wotembereredwa.” Nkulondola uko?

<sup>75</sup> Paulo anali amene anawakakamiza iwo kuti abatizidwenso ngati iwo sanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, “Bwerani ndipo mudzabatizidwenso kachiwiri kuti mulandire Mzimu Woyera,” Machitidwe 19:5. Analinso iyeyo amene anaika manja pa anthu, ndi mphatso, ndipo anawukhazikitsa mpingo mu dongosolo ndi kuchita zozizwitsa, machiritso Auzimu, mphatso za malirime, kutanthauzira kwa malirime. Nkulondola uko? Akorinto Woyamba 12, onani chimene Paulo ananena. Akorinto Woyamba 12, ndipo inu mupeza izo. Iye anaika mu mpingo...Mulungu anaika mu mpingo mphatso zazikulu izi; ndipo Paulo anazikhazikitsa izo mu dongosolo, ndipo anaziika izo mu dongosolo kotero kuti izo zikathe kugwira ntchito kwa ulemelero wa Mulungu. Paulo ananena zimenezo. Ndiye ngati munthu aliyense, ziribe kanthu kuti iye ndi wa chipembedzo chiti, amene adzayesere kukuwuzani inu kuti masiku oyankhula mu malirime, kutanthauzira kwa malirime, Machiritso auzimu, ndi zozizwitsa, ndi umboni wa Mzimu Woyera ngati ubatizo...msiyeni iye akhale wotembereredwa. Pakuti Mzimu womwewo umene unali pa Paulo udzakhala Mzimu womwewo umene unatumizidwa ku m'badwo wa mpingo wotsatira, chomwechonso kwa m'badwo wa mpingo wotsatira, ndi chimodzimodzinso mpaka kumapeto kwa m'badwo wa mpingo. Mzimu womwewo, Mzimu Woyera. Kodi inu mukuhulupirira zimenezo?

<sup>76</sup> Ngati inu mungazindikire izi, izi zinalembedwa apa. Wolembayo ankadziwa. Taonani, “Mizimu isanu ndi iwiri.” Penyani: chilembo chachikulu “M,” Mzimu Woyera, umodzi wokha wa iwo. Uh-huh. Mzimu Woyera womwewo ukubwera kasanu ndi kawiri ku mibadwo yonse isanu ndi iwiri ya mpingo itanyamula Kuwala komweko. Mukumvetsa izo tsopano? Mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, kasanu ndi kawiri Mzimu Woyera uwu ukhala ukunyamula Uthenga womwewu! Umene unalengeza themberero kwa aliyense amene angadzasinthe Iwo.

<sup>77</sup> Tsopano muwone ngati zimenezo zikugwirizana ndi vumbulutso la chinthu chonsecho. Iye anati, “Aliyense amene adzachotse kapena kuwonjezerako, yemweyo adzachotseredwa (gawo lake) kuchoka mu Bukhu la Moyo.” Ndicho chinthu chonsecho chitaphimbidwa pamenepo. Chotero palibe mpata woti inu mudumphe kapena kupanikizika malo ena aliwonse, mwawona, chifukwa ndi Zimenezo. Ndi zomwe Mulungu ananena, ndi zomwe Mzimu unanena, ndipo ndizomwe Mipingo inanena. Tsopano, ngati inu mungayesere kukakamizamo chiphunzitso cha mtundu wina uliwonse chosiyana ndi chimene Paulo anaphunzitsa, izo nzolakwika! Baibulo ndi lolondola. Moyo wake... Yesu anati, “Ine ndidzachotsa gawo lake kuchoka mu Bukhu la Moyo.”

<sup>78</sup> Tsopano, inu mukuti, “Ndi gawo liti la Bukhu la Moyo?”

<sup>79</sup> Pali anthu ambiri amene ali ndi maina awo mu Bukhu la Moyo omwe motsimikizika adzalephera. Inu mukudziwa zimenezo, sichoncho inu? Mukukumbukira kuphunzitsa kumeneko usiku wina uja? Kodi inu munazimvetsa izo? Mwina ndibwereze izo; sizikumvetsetseka bwino pakali pano; sizikumveka bwino, mwaona.

<sup>80</sup> Yudasi Iskarioti anali mwana wa Satana, iye anali mdierekezi akuwonetseredwa mthupi. Baibulo linati iye anali. Baibulo linati, “Iye anabadwa ali mwana wa chitayiko.”

<sup>81</sup> Penyani izi miniti yokha. Tsopano, pa *ichi* panali Yesu; *apa* panali wakuba kumanja Kwake; *apa* panali mmodzi kumanzere Kwake. Tsopano, pamene... Yesu anali Mwana wa Mulungu. Nkulondola uko? Tsopano, anthu ena amangowona mitanda itatu yokha, koma inalipo inayi. Mitanda inayi! Tsopano, kodi mtanda ndi chiyani? Ndi mtengo. Nkulondola uko? Baibulo linati, “Wotembereredwa ndi iye wopachikidwa pamtengo.” Ndipo Iye anapangidwa themberero chifukwa cha ife, Iye anapachikidwa pa mtengo. Iwo unali utadulidwa, koma iwo unali mtengo. Nkulondola uko? Chabwino. Mmusi *apa*, patsinde la phiri, panaima wina. Yudasi anadzzipachika yekha pamtengo wamkuyu. Nkulondola uko?

<sup>82</sup> Penyani! *Apa* pali Mwana wa Mulungu; anabwera kuchokera Kumwamba, akubwerera Kumwamba, atatenga limodzi ndi Iye wochimwa wolapa. *Apa* pali mwana wa chitayiko; anabwera kuchokera ku gehena, akubwerera ku gehena, atatenga limodzi naye (“Ngati Iwe uli!”) wochimwa wosalapa. Mwaona, wochimwa wosalapa, “Ngati Iwe uli Mwana wa Mulungu, dzipulumutse Wekha ndi ifenso.”

<sup>83</sup> Mmodzi *uyu* anati, “Ife tikuye...” (akulalikira, mlaliki wa Uthenga uja) “Ife tikuyenera kulandira zomwe ife tikupezazi, koma Munthu uyu sanachite chirichonse. Ambuye, mukandikumbukire ine pamene Inu mukubwera mu Ufumu Wanu.” Anali ndani ameneyo?

<sup>84</sup> Anali...?... pang’ono pokha usiku watha kapena usiku wadzana. *Uyu* ndi Abele wa Mulungu; *apa* pali Kaini wa mdierekezi. Monga Kaini anapha Abele paguwa lansembe, Yudasi anapha Yesu paguwa. Uko nkulondola. Utsi umangokwera kutali komwe *uko* mu Edeni ndi kudzakhazikikanso pansu pomwe *pano*. Ndizo ndendende.

<sup>85</sup> Oh, ndi zaulemelero, msewu wakale uja, msewu wakale wodala, wongodzaza ndi ulemelero!

<sup>86</sup> Tsopano, tsopano ife tikupeza apa (Ndikhululukireni ine.) kuti mpingo uwu wa Sarde, kwa mngelo, Iye anati, “Mizimu isanu ndi iwiri; Iye amene ali nayo Mizimu isanu ndi iwiri.”

...*kwa mngelo wa mpingo wa Sarde lemba; Zinthu izi anena iye amene ali nayo Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu,...*

<sup>87</sup> Ndipo tsopano ndi angati akudziwa kuti Mulungu ndi Mzimu umodzi? Zedidi. Mulungu, Mzimu Woyera. Mulungu, Atate, Mzimu Woyera, zonsezo Munthu yemweyo, chifukwa Maria anali ndi pakati pa Mzimu Woyera. Tsopano, a . . .koma Mulungu anagwiritsa ntchito Mzimu Woyera uwu mu Kuwala kwaulaliki kusanu ndi kuwiri kosiyanasiyana kwa Mpingo, mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Mukumvetsetsa zimenezo? Mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo.

<sup>88</sup> Tsopano, inu mukuti, “Mulungu samachita zimenezo.” Oh, inde, m'bale.

<sup>89</sup> Taonani! Iye anagwiritsa ntchito Mzimu wa Eliya, ndipo pamene Elisha anachokapo . . . Eliya atachokapo, Elisha analandira magawo awiri a Iwo. Ndipo pamene Elisha anadzadwala ndi kufa, ndiye Iwo unabwereranso kachiwiri pa Yohane M'batizi. Chinthu chomwe chomwecho, chinamupangitsa iye kumachita chimodzimidzi monga Eliya ankachitira, akukhala mwa chipululu ndi zina zotero. Nkulondola uko? Ndipo ananeneratu kuti udzabweranso mu masiku otsiriza, mwaona. Mulungu amagwiritsa ntchito Mzimu kudutsa monsemo.

<sup>90</sup> Ndipo Yesu anadzozedwa ndi Mzimu Woyera, ankayendayenda akumachita zabwino. Nkulondola uko? Ndipo Mzimu Woyera womwewo unali pa Yesu, unadzabwereranso mu Mpingo pa Tsiku la Pentekoste, kubwereranso kudzalowa mu m'badwo wotsatira, m'badwo wotsatira, m'badwo wotsatira. Ndipo Iwo ndi chiyani? Mzimu Woyera womwewo ndipo umodzi womwewo. Oh, kodi inu simukuwona? Mulungu pamwamba pathu, mwa Atate; Mulungu ndi ife, mwa Mwana; Mulungu mwa ife, mwa Mzimu Woyera. Ndi maofesi atatu, osati amulungu atatu. Mukuona? Ndipo maudindo atatu amenewo (Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera) ndi a Dzina limodzi: Yesu Khristu. Chabwino.

<sup>91</sup> Tsopano, penyani tsopano pamene ife tikupitirira. “Mizimu isanu ndi iwiri,” atero Iye amene akugwira . . . Mwakulankhula kwina, “amawagwira amithenga Ake.” Amithenga omwe adzazozedwe ndi Mzimu Woyera, ndi Mzimu Woyera womwewo umene Paulo (woyambayo) anadzozedwa nawo, wachiwiri, wachitatu, wachinayi, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, ndi wachisanu ndi chiwiri, onsewo ali mdzanja Lake lamanja. Oh, akutenga mphamvu zawo ndi Kuwala kwawo kuchokera ku dzanja Lake lamanja.

<sup>92</sup> Tsopano, Iye anakwera Mmwamba. Ndipo Filipino anati, pamene iye ankafa . . . Kapena Stefano anati, “Ine ndikuwona kumwamba kutatseguka, ndipo . . . ndipo Yesu wakhala padzanja lamanja la Mulungu.” Zimenezo sizikutanthauza kuti Mulungu ali ndi dzanja lamanja lalikulu ndipo Iye wakhala

pamenepo, koma *dzanja lamanja* zimatanthauza dzanja lamanja la “mphamvu ndi ulamuliro.”

<sup>93</sup> Thupi lija limene Mulungu analilenga... “Sindidzalola Woyera Wanga Uyo kuti awone chivundi, komanso Ine sindidzasiya moyo Wake mu gehena, koma ndidzamuukitsa Iye ndi kudzamukhazika Iye mmalo mwa Mzimu pa guwa.” Penyani! Pamene iwo amuwona Iye—Iye atakhala paguwa, ndipo anali nalo Bukhu mdzanja Lake, ndipo panalibe munthu padziko lapansi kapena pansu pa dziko, kapena kulikonse, anali wokhoza kapena woyenera ngakhale kuliyang’ana Bukhulo; koma Mwanawankhosa yemwe monga Iye wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi, kumbuyo komwe ku chiyambi pamene Iye anayamba kuganiza za thupi lowomboledwa ili, anabwera ndipo anadzalitenga ilo kuchokera mdzanja lamanja la Iye amene amakhala pa Mpandowachifumu, ndipo anadzakhala pansu, Iyemwini. Amen. Ndi zimenezotu. Malemba ake ndi amenewo. Izo ndi zokongola basi, mwaona.

<sup>94</sup> Tsopano, “Iye amene agonjetsa adzakhala ndi Ine pa Mpandowachifumu Wanga, monga Ine ndagonjetsa ndipo ndakhala pa Mpandowachifumu wa Atate Anga.” Mwakulankhula kwina, “Ine ndinatengera mthupi Langa momwe Mzimu Woyera. Ine ndinagonjetsa zinthu zonse za padziko lapansi (kudzera mu yesero) mwa Mzimu Woyera, ndipo ndinalanda!” (“Ndipo mwa Iye mukukhala chidzalo cha Umulungu mthupi.”) “Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zapatsidwa mmanja Mwanga,” Iye anatero. Mphamvu zonse! Ndiye kuti Mulungu alibe mphamvu ngati Iye ali munthu wina. Pakuti Baibulo linati, Yesu anati, chitachitika chiukitsiro Chake, kuti “Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi, zonse ziwiri, zinaperekedwa mdzanja Langa.”

<sup>95</sup> Ndipo Yesu akubwera kuchokera Kumwamba ndi Oyera Ake teni sauzande kuchulukitsa ndi teni sauzande, ndipo Baibulo limanena kuti “Miyamba inali yopanda kanthu kwa theka la ora.” Ali kuti Munthu wamkulu uyu, Mulungu, ndiye? Uh-huh. Mukuona? Iye ali mwa Khristu. Ndithudi! Ndipo pamene ife tigonjetsa mwa Mzimu Woyera monga Iye anachitira, ife tidzakhala ndi Iye pamene Iye azidzatenga mpando wachifumu wa padziko lapansi wa Davide, kudzakhala ndi kudzalamulira ndi Iye monga momwe Iye anachitira Kumwamba uko, (Amen!) ndi mphamvu ndi ulamuliro pa dziko lonse lapansi. “Ndipo iwo ali. . . dziko lapansi likubuula, kuyembekezera mawonetseredwe a ana aamuna a Mulungu kuti awonetseredwe, mwana wa Mulungu.”

<sup>96</sup> Chifukwa, kuwonjezera apo, dziko ili silinaperekedwe kuti Mulungu azililamulira. Tiyeni tizindikire kuti zimenezo ndi zoon. Kodi mulungu wa dziko lapansi ndi ndani? Munthu! Ndiwo ulamuliro wake. Zonse, chirichonse padziko lapansi chimamumvera munthu. Kudzera mu tchimo iye

anagwa; kudzera mu mphamvu yowombola ya Khristu iye akubwereranso kachiwiri. Uko nkulondola, chifukwa dziko lapansi ndi la munthu, ilo linaperekedwa kwa iye ndipo iye anali wolamulira pa chirichonse. Ndipo chirengedwe chonse chikubuula, kuyembekezera nthawi imeneyo pamene ana aamuna a Mulungu adzawonetseredwe kachiwiri. Oh, ine; oh, mai! Mawonetseredwe a ana aamuna a Mulungu. Tsopano, ife kulibwino tizisiye izo pakali pano.

<sup>97</sup> Koma, amithenga ali mdzanja Lake lamanja, akudikirira, kulikonse komwe Iye angawatumizeko iwo, iwo adzayankhula chinthu chomwecho, pakuti Mzimu Woyera umene unali mwa Khristu... Oh! Mzimu umene unali mwa Khristu! Pamene Iye anachoka, Iye anati, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko lapansi,” *kosmos*, mawu a chigriki omwe amanthauza “dongosolo la mdziko,” osati dziko lapansi, mdziko, dongosolo la mdziko, “silidzandiwona Ine kenanso,” zipembedzo, kapena zina zonsezo, “silidzandiwona Ine kenanso, komabe inu mudzandiwona Ine,” Mpingo, wokhulupirira, “pakuti Ine,” *Ine*, puronauni yaumwini ndi yolondola, “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, kufikira chimaliziro cha dziko lapansi. Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse.” Inu mukuziwona Zimenezo?

<sup>98</sup> Ndiye ngati umenewo unali Mzimu Woyera wa Khristu unabwera pa Tsiku la Pentekoste womwe unkachita zinthu zimenezo, ndi Mzimu Woyera wa Khristu umene wakankhidwira kunja *kuno*, Mzimu Woyera wa Khristu ukugwiritsitsabe *muno*, Mzimu Woyera wa Khristu ukugwiritsitsabe *pano*, mpaka mmunsi *apa* mpaka kumathelo a dziko lapansi. Mzimu Woyera womwewo umene unamudzaza Paulo ndi Mzimu Woyera ndi zinthu zomwe iye anazichita, udzamuzadza mmodzi *uyu* (Ireniasi) wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, udzamuzadza Martin wozadza ndi Mzimu Woyera, ukuwazadza ena onsewo kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo Iwo unakuzadzani inu ndi ine kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo iwo ndi Madalitso Achipentekoste ochokera ku m’badwo wina wa mpingo kupita kwa umzake; Alfa ndi Omega, Mapeto ndi Chiyambi, ndi Zonse, Muzu ndi Mphukira ya Davide, Nyenyezi Yammawa, Duwa la Sharoni, Kakombo wa Mchigwa, china chirichonse, Atate, Mwana, Mzimu Woyera, Iye amene Anali, Amene Ali, ndi Amene Adzabwera, Alfa, Omega, Zonse, Zonse mu Zonse! Oh, mai! Izi zitha kundipangitsa ine kuyimba nyimbo:

Oh, Mukunena kuti Ine ndine ndani, (anatero Yesu,) mumanena kuti Ine ndinachokera kuti,  
Kodi inu mukuwadziwa Atate Anga, kapena kodi inu mungalidziwe Dzina Lawo?

Iye anati: Ndine Alfa ndi Omega, woyamba kuchokera kumapeto, INE NDINE chirengedwe chonse, ndipo Yesu ndiro Dzina.

INE NDINE amene analankhula kwa Mose mu chitsamba chonyeka Moto, INE NDINE Mulungu wa Abrahamu, Nyenyezi Yowala ndi ya Mmawa. (Uko nkulondola.)

INE NDINE Duwa la Sharoni, ndipo munati Ine ndinachokera Kuti?

INE NDINE chirengedwe chonsecho, koma Yesu ndiro Dzinalo.

<sup>99</sup> Banja lonse Mmiyamba ndi dziko lapansi limamangirizika mu limodzi limenelo (lapadziko lonse, lodala, lodzazidwa Mzimu Woyera, lolumphira pansi, lotchulidwa ndi Mzimu Woyera, loyankhulidwa ndi Mzimu Woyera, lobadwa mwa Mzimu Woyera) Dzina. Uko nkulondola. Mulungu analipereka Ilo kwa banja lonse Kumwamba ndi dziko lapansi. Ndipo chirichonse mmenemo, bondo lililonse, lidzagwadira pa Dzina limenero. “Ndipo palibe Dzina lina loperekedwa pansi pa Kumwamba limene anthu ayenera kupulumutsidwa nalo.” Osati *mwinamwake*, *akuyenera kutero*, koma *ayenera* kupulumutsidwa. Oh, ine ndikulikonda Ilo. Ilo basi ndi labwino. Chabwino.

<sup>100</sup> “Mu dzanja Lake lamanja.” Tsopano kodi inu mukufufuza? Ndi Mpingo wa pentekoste; mphamvu, zizindikiro, zodabwitsa zikuchitika njira yonse. Tsopano ndife. . . Tinapita kudutsa kupyola Mibadwo ya Mdimu kumene Iwo unali pafupi kuti uzimitsidwepo. Tsopano tiyeni titenge ndime iyi ya 2. Oh, ine ndikukhulupirira kuti ife tizingopitirira basi pa—pang’ono pokha ndi iyi ya 1 panobe:

*. . . Ine ndikudziwa ntchito zako, kuti iwe uli nalo dzina lakuti uli ndi moyo, ndipo ndiwe wakufa.*

<sup>101</sup> Tembenuzirani ku mpingo wotsatira apa, inu mupeza, “Koma iwe sunakane dzina langa.” Kutsatira mpingo, “Sunakane dzina langa.” Koma mu mpingo *uwu*, “Iwe uli nalo dzina.” Taonani apa! Mpingo *uwu* unasunga Dzina Lake; mpingo *uwu* unasunga Dzina Lake; mpingo *uwu* unasunga Dzina Lake; ndipo mpingo *uwu* unadutsa mu M’badwo wa Mdimu ndipo panalibe chimene chinanenedwa cha iwo; pamene iwo anatulukuka kupita ku Moyo ku mbali *iyi*, woyamba wamng’ono wopulumukayo, pamene Luther anawatulutsa iwo kunjira, “Iwe uli *nalo* dzina kuti uli wamoyo, koma iwe ndi wakufa.” Tsopano, ndi dzina liti limene iwo ankalgwiritsa ntchito atasiya kugwiritsa ntchito Dzina la Yesu? Atate, Mwana, Mzimu Woyera.



Ndipo apo palibepo chinthu choterocho. Ndi zakufa—ndi fioloje yakufa.

<sup>102</sup> Ndiuzeni ine, kodi Atate ndi dzina? Ndi atate angati omwe ali muno? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndani wa inu dzina lake ndi Atate? Ana? Ndipo anthu? Ndizo—ndizo zomwe izo ziri. Si zimenezo . . . Dzina Lake si Mzimu Woyera, ndi chomwe Iwo uli; Iwo *ndi* Mzimu Woyera. Dzinalo . . . Mzimu Woyera si dzina, Mzimu Woyera ndi udindo; Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.

<sup>103</sup> Chotero inu mukuwona pamenepo, zopanda popondera monga umwana Wamuyaya. Palibepo chinthu chonga umwana Wamuyaya. Mwana amabwera kudzabadwa; Wamuyaya samatero nkomwe.

<sup>104</sup> Kulibeko chinthu choterocho, monga ine ndinanenera usiku wina, ngati gehena Yamuyaya. Kodi mungaipeze bwanji gehena Yamuyaya? Nthawizonse kunali kuli gehena, ndiyetu. Baibulo linati, “Iyo inalengedwera mdierekezi ndi angelo ake.” Nthawizonse padzakhala pali gehena; ngati imozi itidzakhale ilipo nthawizonse, payenera kuti inalipo imodzi pachiyambi. Ndipo chiyani. . . Ndani ankaigwiritsa iyo ntchito kumbuyoko pamene—pamene Iye anali *El, Elah, Elohim*, “Iye wokhalapo yekhayo,” pamene kunalibe chirichonse? Ndiye gehena iyenera kuti inali ndi Iye kumeneko. Mukuona? “Gehena inalengedwera mdierekezi ndi angelo ake. Ndipo oipa onse adzaponyedwera mmenemo.” Ndizo ndendende kulondola. Iwo adzalandidwa mwinamwake kwa zaka handiredi miliyoni chifukwa cha zomwe iwo anachita. Koma idzafika nthawi yomwe iwo adzakhale ndi imfa yachiwiri. Sipadzakhala chirichonse chomwe chidzatsalire cha iwo. Chirichonse chomwe chinali ndi chiyambi chiri ndi mathero. Chotero pamene ife tikulandira Moyo Wamuyaya, ife tikulandira gawo la kuwala kwa mdziko kumene kunali kumbuyo uko pasanakhalepo konse molekyu. Uh-huh. Kuwala kumeneko kwa Mulungu kumabwera mumtima mwathu kumene kumatiunikira ife kuti ife tizimuwona Yesu. Baibulo linati, “Ife sitimawona zinthu zonse, koma ife timamuwona Yesu.”

<sup>105</sup> Tsopano, Iye anati, “Ine ndikudziwa ndi amene. . . Ine ndine Iye amene ndiri ndi Mizimu isanu ndi iwiri yomwe yatumizidwa ku mipingo isanu ndi iwiri. Ine ndikudziwa ntchito zako zonse ndi zonse zokhudza izo, koma iwe uli nalo dzina kuti ndiwe wamoyo koma ndiwe wakufa.” Tsopano, inu mukukumbukira; unali m'badwo wa ndani uwu? Martin Luther, m'badwo wa Chilutera. Tsopano, iwo anaweruzidwa poyamba. Iwo sankasowekera ngakhale kuti ayambe nkomwe, iwo anali akufa kuyamba ndi kuyamba. Iwo sankasowa kuti afe, iwo anali akufa kuyamba ndi kuyamba. Mwaona, iwo basi “anangolanditsidwapo.”

<sup>106</sup> Tsopano zindikirani izi. Tsopano tiyeni tiwerenge ndime yotsatira:

Penyani! *Khalani atcheru, ndipo mulimbikitse zomwe zatsalira, zomwe ziri pafupi kufa: pakuti Ine sindinazipeze ntchito zako kukhala zangwiro pamaso pa Mulungu.*

<sup>107</sup> Tsopano, iye akuyankhula ndi Luther tsopano. Ife tonse tivomereza kuti uwu—uwu unali m'badwo wa Chilutera, uko kunali kukonzanso. Tsopano kodi Iye ananena chiyani? “Inu munatulutsa dzina labodza kuti ndinu ‘amoyo,’ koma ndinu akufa.” Kodi iwo anachita chiyani? Iwo analiyikanso ilo mu chipembedzo kachiwiri. Ndiye, “m’phika sungatchule ketulo ‘noninoni,’” musamunene, “Mkatolika!” Mwaona, chifukwa inu mwabwerera kumene mmenemo, mukugwiritsa ntchito tizikhulupiriro take tomweto ndi maina. Ndipo, chabwino, Luther anabweretsa makatekisimu ambiri ndi china chirichonse zimene mpingo wa Katolika unali nazo, ndipo anadzitengera okha dzina. Mwaona, “Inu muli nalo dzina loti ndinu ‘amoyo,’ omwe mwachokera ku zaka sauzande zakufa kuno, ndipo inu mukugwiritsitsabe dzina limenero.” “Inu muli *nalo* dzina,” mukukumbukira?

<sup>108</sup> Kukhala otsimikiza kuti zimenezo ndi zoono, mipingo inayo, anati, “Inu mwasunga Dzina Langa.” “Inu mwasunga Dzina Langa.” Mu m'badwo *uwu* iwo “analitaya Ilo.” Ndipo anatulukira *kuno* ndipo anati, “Inu muli ndi dzina lina lakuti ndinu ‘amoyo,’ koma ndinu akufa.”

<sup>109</sup> Oh, inu Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Achilutera, ndi Pentekoste, lapani ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu. Mukuona? Chokaniko ku tizikhulupiriro takale takufa ndi zinthu zomwe ndi za mpingo wa Katolika zomwe zidzawonongedwa ndi ana ake onse aakazi ndi izo.

<sup>110</sup> Palibe aliyense amene anganene kuti “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” iwo ali ngati...Ndi chinthu chimenecho, ndipo iwo amachitcha “Utatu Woyera.” Utatu? Ine ndikufuna winawake kuti apeze ngakhale mawu akuti *utatu* mu Baibulo, ndipo abwere adzandiuze ine za izo, mungopeza mawu akuti *utatu*. Mulibemo nkomwe mmenemo. Mulibemo chinthu choterocho.

<sup>111</sup> Tsopano, tsopano:

. . . ndi *wokonzeka kufa*: . . .

<sup>112</sup> “Gwiritsitsani kwa icho chimene inu muli nacho, Luther anakulandani inu. Gwiritsitsani kwa chimenecho, chifukwa icho chakonzekera kufa. Inu mudzatero. . . Iwo adzakuyereetsani inu mmenemo kachiwiri. Gwiritsitsani kwa icho, icho chakonzekera kufa.”

<sup>113</sup> Tsopano:

...ndipo *Ine sindinakupeze* iwe wangwiro panobe  
*pamaso pa Mulungu.*

114 Kodi zimenezo si zokongola? Oh, mai! Ine ndimazikonda zimenezo. “Osati wangwiro.” Chifukwa chiyani? Iwo anangolungamitsidwa chabe, Luther analalikira kulungamitsidwa; iwe umayenera kuti uyeretsedwe ndipo kenako udzazidwe ndi Mzimu Woyera. Ndiyeno iwo sanali a iwoeni, iwo anapangitsidwa kukhala angwiro ndi Mzimu Woyera mwa iwo. Samakhala—samakhala Mkhristu yemwe amakhala wangwiro, ndi Mzimu Woyera wangwiro mwa iye. Mukuona? Ndizo zomwe...Monga ine ndimanena, “Si phiri loyera, ndi Mulungu Woyera pa phirilo. Si mpingo woyera, si anthu oyera, koma ndi Mzimu Woyera mu Mpingo ndi mwa anthu.” Ndiro gawo *Loyera*, mwaona.

115 “Ndipo ine sindinazipeze ntchito zanu kukhala zangwiro. Inu simunabwere ku ungwiro.” Chifukwa ife tikupeza tsopano kuti iwo anali nako kulungamitsidwa pomwe *apa*, kulungamitsidwa. Ndipo izi zinali...Ayi, ine ndikupempha chikhululukiro chanu. Kulungamitsidwa kuli pomwe *apa* pansi pa Luther; ndipo kuyeretsedwa kuli *apa*; ndipo *apa* pali Mzimu Woyera. Mukuona? Tsopano, zinthu zitatu zimenezo zimene zinkagwira ntchito mu mibadwo itatu ya mpingo imeneyo, ndizo zomwe zimatengera kuti zipange kubadwa kwathunthu. Iwo anabalidwa ngati kanyongolosi kakang’ono mmimba mwa amayi. Ndiko kulondola, Mzimu Woyera ukufika pa kubadwa.

116 Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake. Pamene kubadwa kwachirengedwe kuchitika, chinthu choyamba chimene chimachitika ndi chiyani? Madzi. Chinthu chotsatira? Magazi. Kulondola uko? Chinthu chotsatira? Mzimu. Uko nkulondola.

117 Chinatuluka ndi chiyani mthupi la Yesu pamene Iye ankafa? Iwo anamupyozza mnthiti Mwake, ndipo madzi ndi Magazi zinatulukamo, “Ndipo mmanja Mwanu Ine ndikupereka Mzimu Wanga.” Madzi, Magazi, Mzimu.

118 “Chotero polungamitsidwa mwa chikhulupiriro,” Aroma 5:1, “ife timakhala ndi mtendere ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu,” kulungamitsidwa. Kuyeretsedwa, Ahebri 13:12 ndi 13, “Yesu anazunzika kunja kwa zipata kuti Iye akakhoze kuyetsa anthu ndi Magazi Ake Omwe.” Luka 24:49, “Koma dikirani inu mu mzinda wa Yerusalemu kufikira inu mutadzazidwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba. Zikadzachitika izi Mzimu Woyera udzabwera pa inu, *kenako* inu mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, Yudeya, Samaria...”

119 Osati pamene inu munadzakhala bishopu, osati pamene munadzakhala dikoni, osati pamene munadzakhala m’busa, osati pamene munadzakhala papa, “Koma zikadzachitika kuti

Mzimu Woyera wabwera pa inu, ndiye inu muzidzachitira umboni.” Inu mukhoza kokha kuchitira umboni za mpingo wanu ndi za kachikhulupiriro kanu, monga a . . . ngati mwangokhala dikoni, kapena ngati inu mwangokhala m’busa, kapena ngati inu mwangokhala papa, kapena ngati inu muli . . . Inu mukuchitira umboni za kachikhulupiriro! Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera, ndiye inu mudzachitira umboni za Iye! Ndipo ntchito zimene Iye ankachita, inunso mudzazichita, chifukwa Moyo Wake uli mwa inu. Oh, oh! Mai, mai! Monga choncho. Inde, bwana. Oh, ine ndimawupeza iwo wochuluka wa Iwo pamwamba apa, ine ndikukhulupirira, kuposa momwe inu mumachitira kunja uko. Ine ndimangomverera bwino nawo Iwo.

<sup>120</sup> “Zinthu zomwe zakonzeka kuti zife, gwiritsitsani kwa izo.” Tsopano iye akunena apa, tsopano mu ndime ya 3:

*Kumbukirani chotero momwe inu munalandirira ndi kumva, (Ine ndikuzikonda zimenezo.) ndipo mugwiritsitse zolimba, ndipo mulape. Ngati chotero inu simuyang’anira, ine ndidzabwera kwa inu ngati mbala, ndipo inu simudzadziwa ora limene ine . . . ndidzabwera pa inu.*

<sup>121</sup> “Gwiritsitsani ku kulungamitsidwa kwanu, kangamirani kwa iko.” Musalole kuti anthu amenewo asungunulire iko m’mbuyo kutali ndi inu. “Kuti pameneponso inu munalandira, inu munazimva.” Iwo amawerenga Baibulo lomwelo limene ife timawerenga, mwaona. Koma iwo sanangotenga zonse za Ilo, chifukwa Ilo silinawululidwe kwa iwo. Ilo silinali la m’badwo wawo. Ndi chifukwa chake iwo adzatulukira mu chiwukitsiro. Iwo anayenda mu Kuwala kumene iwo amayenera kuti aziyendamo, chotero iwo adzatulukira.

<sup>122</sup> Tsopano, ine ndamvapo anthu ambiri Achipentekoste omwe amalalikira ubatizo, akuti, “Achilutera amenewo, ndi ena otero, sadzatulukira.” Oh, inde. Inu mukudziwa kankhani kakang’ono kokhudza Dr. Hegre kumtunda uko. Pamene ine ndinamuuza iye . . . Iye anati, “Ndife chiyani?” Ine ndinati . . . Inu mukudziwa, iwo anamanga seminare yayikulu ya Chilutera imeneyo kumeneko, Bethany, ku Minneapolis. Ndipo iye anati, “Chabwino, ndi chiyani chimene ife tiri nacho chimene Achilutera ali nacho?”

Ine ndinati, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu. Ine ndikukhulupirira inu muli ndi Khristu.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, ife tikufuna—ife tikufuna Mzimu Woyera.” Iye anati, “Kodi inu mukuganiza kuti ife tiri nawo Iwo?”

Ine ndinati, “Mwanjiraina.” Ndipo ine ndinati, “Inu mukukhulupirira poyang’ana kwa Iwo.”

Iye anati, “Chabwino, inu mukutanthauza chiyani?”

123 Tsopano, iwo ali ndi maekala masauzande kumeneko omwe ophunzira awo. . . ngati iwo sangathe—sangathe kulipira njira yawo yonse, iwo amawalola iwo kuti agwirire ntchito njira yawo yonse ndi kulima chimanga. Ine ndinati, “Chabwino. . .” Pali basi—matebulo akuluakulu okha. Iwo anandipatsa ine chimodzi cha chakudya chankhomaliro chamadyo ichi kumusi uko ku seminare yaikulu ija. Ndipo tsopano, iwo ndi amuna abwino; Dr. Hegre akhala *apa*, ndi M'bale Jack Moore cha *apa*; chifukwa ine ndinamuyika iye pafupi kuchitira kuti ngati iye atayamba kuyankhula mawu ena aakulu omwe ine sindikuwadziwa, ine ndimugunyuze Jack ndi mwendo wanga ndikuwona zomwe iye wanena, inu mwaona. Chotero ndiye, ine ndinati. . .

124 Iye anakhala pafupi ndi ine, ndipo iye anati, “Chabwino, zomwe ife tikufuna kuchita ndikupeza chinachake apa.” Anati, “Ife tiri ndi njala ya Mulungu.” Ndipo anati, “Ife tinawerenga bukhu la Pentekoste, *Mphatso*.” Ndipo anati, “Ife tinapita. . . gulu la abale ife tinapita ku California, ife tinakakumana ndi munthu amene analemba bukhulo.” (Ndipo ine ndikumudziwa iye.) Iye anati, “‘Ife tikufuna kuwona mphatso zina zikugwira ntchito.’ Iye anati, ‘Ine ndiribe iliyonse ya izo,’ anati, ‘Ine ndinangolemba za izo.’” Chotero iye anati. . . Ndipo anati, “Kenako pamene ife tinabwera kumeneko ndipo ife tinawona izi, ife tiri ndi njala. Ife tikufuna Mulungu.”

125 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, nthawi ina panali munthu anatuluka.” Inu mukudziwa, ku malo ake omwe kumeneko, inu mwaona. “Munthu anapita ndipo anakagalauza munda waukulu kwambiri. Ndipo anakusamo mizu yonse mmenemo, ndi chirichonse, ndipo kenako iye anabzalamo chimanga. Mmawa uliwonse iye ankapita pakhomu ndi kumakasuzumira kuti awone ngati iye anali ndi chimanga chirichonse. Chinthu choyambirira inu mukudziwa, mmawa wina, timasamba tiwiri tinatulukira pamwamba.” (Aliyense amene anayamba walimapo chimanga. . . Ali kuti George Wright ndi iwo, Roy Slaughter ndi iwo? Inu mukudziwa, timasamba tiwiri tija tomwe timatulukapo.) “‘Oh,’ iye anati, ‘Mulungu alemekezeke chifukwa cha munda wanga wa chimanga.’”

Ine ndinati, “Kodi iye anali ndi munda wa chimanga?”

Iye anati, “Chabwino, mwanjira ina.”

126 Ine ndinati, “Mwakunena kwina, inde.” Ine ndinati, “Amenewo munali inu Achilutera mu kukonzanso koyamba, kuphuka tsamba laling’ono limenelo, mwaona.” “Chabwino,” Ine ndinati, “pang’ono ndi pang’ono chimanga chimenecho chimakula.” Ine sindinamuuze iye za “kugwa,” inu mwaona, ine ndinangomusiya iye azipita ndi chimangacho, chikukula.

127 Chotero ine ndinati, “Chimangacho chimakula, ndipo patapita kanthawi chinadzakhala ndi ngayaye pa icho. Ndipo ngayaye imeneyo inayang’ana mmbuyo ku tsamba ndipo inati,

‘Ha-ha-ha-ha-ha, iwe ulibe kalikonse, inu Achilutera akale ofunda.’ Mukuona? Anati, ‘Ine ndine . . . Ine—Ndine wobereketsa, nthawi yaikulu ya umishonare.’ Mphepo imawomba, ndipo ngayaye zazing’ono zimagwa monga choncho ndipo zimagwera pansi; ameneyo ndi Wesley, kuyeretsewa.” Mukuona? Umenewo unali m’badwo wopambana kwambiri waumishonare umene tinayamba takhalapo nawo, wakhala uli mpingo wa Wesile, mu nthawi ya Wesley, ikuposa ngakhale m’badwo uno. M’badwo wa Mpingo wachi Wesley, iwo unali m’badwo wa umishonare, ndipo iwo unamwaza. Kodi iwo unachita chiyani, iwo—iwo unawamwaza Iwo.

<sup>128</sup> Mwaona, ngakhale chirengedwe chimachitira umboni za atatu awa, pomwepo apo. Chirengedwe chokha, Mulungu pachiyambi anazipanga izo chomwecho kuti zizikhala mwanjira imeneyo. Inu simumasowa ngakhale kuti mukhale ndi Baibulo, inu mukhoza kuyang’ana pa chirengedwe ndi kuwona komwe inu muli. Mukuona?

<sup>129</sup> Ndiyeno . . . Ndipo pamenepo patapita kanthawi zinagwera kumeneko. Ndipo panatuluka chiyani? Apo panadzabwera ngala ya chimanga, iyo inali ndi njere pa iyo; limenelo linali gulu la Chipentekoste. Tsopano, gulu la Chipentekoste linali mtundu womwewo wa gulu kumusi *kuno*. Kuchokera *apa* iye anali ndi masamba awiri a chimanga, Luther; *apa* iye anali ndi ngayaye, Wesley; ndipo pamusi *apa* iye anali ndi mbewu ya chimanga (Chiyani?) ndendende basi yonga yomwe inali kumbuyo *uku*. Chinthu chomwe chomwecho!

<sup>130</sup> Chabwino tsopano, chinali chiyani ichi apa? Inu mukuti, “Chabwino, tsopano,” Achipentekoste anati, “ine ndiribe nanu ntchito inu Amethodisti kapena inu Achilutera.” Koma, kuwonjezera apo, moyo womwewo umene unali mu timasamba tiwiri tating’ono ito unathandizira kupanga ngayaye. Ndipo moyo unali mu ngayaye unapanga chimanga. Chotero, inu mwaona, yonseyo ndi purogramu ya Mulungu. Iwo anali ndi Mzimu Woyera, mwakunena kwina; chomwechonso Wesley anatero, pansi pa kuyeretsewa; koma lero izo zinabweretsanso kuyankhula mmalirime ndi kubwezeretsa kwa chiyambi kumbuyo *apa*. Mzimu Woyera womwewo, inu mukuona, iwo owonawo. Ameni. Inde.

<sup>131</sup> Chabwino, “Gwiritsitsani chimene inu mwamva, kuwopa kuti chingafe.” Tsopano ndime ya 4, ine ndikukhulupirira ndi imeneyo:

*Iwe uli nawo mayina apang’ono ngakhale mu Sarde omwe sanadetse zovala zawo; ndipo iwo adzayenda ndi ine mu zoyera: pakuti iwo ndi oyenera.*

<sup>132</sup> “Tsopano, musapange chipembedzo mwa Iwo, ife sitikufuna kuti tichite zimenezo.” Ayi, ine nda . . . ine—ine ndinawerenga ndime yolakwika, sichoncho ine? Kapena ine sindinatero?

Eya, eya, uko nkulondola. Eya. Chabwino. Eya, “Mu Sarde, sanadetse zovala zawo.” Munali owerengeka a iwo amene sanakagwadirebe chinthu chimenecho, ndipo anadzisunga okha angwiro ndi oyera; zikhalidwe zakale kuchokera komwe kutali mmbuyo ku Pentekoste, odzazidwa ndi Mzimu. Ambiri a iwo ndiye, pamene m'badwo wa Lutera unayamba kupanga chipembedzo; kodi iwo anachita chiyani? Anayambiranso mmbuyo momwe Baibulo linanenera, “Kumachita ngati amayi wawo.” Anabwerera mmbuyo momwe, anayambitsa chipembedzo. Koma ochepa a iwo anayimirira poyera kuti iwo sangachite zimenezo, iwo anakhalabe molondola ndi Mulungu. Anati, iwo anati—anati, “Chabwino, chabwino, inu muli nawo maina ochepa, ndipo ndi oyenera kuyenda pamaso Panga, atavala zoyera. Musapange chipembedzo. Musatenge chiphunzitso cha Chinikolai, tsopano. Musayambitsenso chipembedzo chanu kenanso, koma mungokhala amfulu mwa Mulungu. Mulole Mzimu Woyera uzikutsogolerani inu pamene mukupitirira. Alipo ochepa a iwo omwe atsalirabe.”

133 Tsopano ndime ya 5, ine ndikukhulupirira:

*Iye amene ali ndi khutu, muloleni iye- . . .*

134 Tiyeni tiwone. Ayi.

*Iye amene agonjetsa, yemweyo adzavekedwa zovala zoyera; ndipo Ine sindidzafufuta...dzina lake kuchokera mu bukhu la moyo, koma Ine ndidzavomereza dzina lake pamaso pa Atate anga, ndi pamaso pa angelo.*

135 Tsopano, “maina apang’ono.” Apang’ono kwambiri, wotsalira wapang’ono, anatsalira omwe sanatenge... kutenga... anachenjereredwa ndi chiphunzitso cha Katolika. Chabwino.

136 Tsopano ife tafika poyankhula za kukonzanso. Ine ndikufuna kuti...ine ndinalenzeza pa maziko a Luther kuti ndizitengere izo umu apa. Tsopano ndime yotsatira inati:

*Iye amene ali nalo khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo.*

137 Mulungu, kuyesetsa kuti awachenjeze iwo apa kuti akhale kunja kwa Chinikolai ichi, “Khalani kutali ndi kumeneko! Sungani zovala zanu zopanda banga muchoke ku zinthu zirizonse zachidziko!” Mukhale amfulu mwa Iye, ndipo Iye akanadzawatsogolera iwo ndi kuwalondolera iwo. Tsopano, ndicho chiyambi choyamba.

138 Tsopano, ndi *kukonzanso* ine ndikutanthauza “opulumukawo,” omwe anapulumuka ngakhale mu mpingo wa Sarde. Kodi inu mukumvetsa zomwe ine ndikutanthauza? Iwo omwe anali atapulumuka chinthu chowopsya chimenecho. Tsopano izo...Tsopano, ife tidzazitenganso izo mawa usiku

ndi kuzibweretsa izo mpaka kuno mu . . . kulowa mu m'badwo wa Pentekoste, ndi kukuwonetsani inu kuti ndizo ndendende. Tsopano, pali zina za zinthu zimenezi, zimene ife timakambirana apa: “Kodi iwo anapululumuka chotani izo?” Tsopano, ife tidzazitenga izo, uko mu m'badwo wotsatira. Mwaona, ife tiyenera tidzazitenge izo kuti tidzazipange izo kuyendera limodzi. Ngati inu simutero, ndiye kuti inu—inu—inu—mwaphonya kupereka—anthu . . . kukhomera iwo mu m'badwo wotsatira uwo, inu mwaona. Inu mukuyenera kuwalola iwo kuti akhale nazo izo monga momwe Baibulo limaperekera izo apa, mwaona. Chabwino.

<sup>139</sup> Tsopano, opulumukawo ndi amene Iye akuwakamba. Ndi awa pomwe *apa*, kagulu kakang'ono aka komwe kakhala moyo wolungamitsidwa. Tsopano taonani! Iwo anatuluka, iwo anawona Kuwala, Luther anatembenukira kumanja . . . Pambuyo pa imfa ya Luther, osati Luther; Luther sanapange konse bungwe lirilonse; linali gulu lija la pambuyo pa iye. Wesley sanapange konse bungwe; linali gulu lija la pambuyo pa iye. Oyambitsa akale awo a Pentekoste sanapange konse bungwe; linali gulu lija la pambuyo pa iwo. Iwo ndi amene amachita zimenezo, mwaona, ndi kuzungulira kwachiwiri kumene kumachita zimenezo. Mngelo weniweni wa Kuwala sadzapanga konse bungwe! Ndipo inu mudzapeza pa uwu—pa m'badwo wa Pentekoste uwu zomwe zikudzabwera kumapeto kwa bungwe limenelo, nazonso; mwawona, pamene Mzimu Woyera uwulula izo kwa ife.

<sup>140</sup> Tsopano, Iye anati, “Muli nako Kuwala kwapang'ono kwatsalira, pang'ono pokha, Iko kwatsala pang'ono kufa; iko kukufota, ndiko kulungamitsidwa basi, iwo akhoza kukuzunguzani inu kulikonse. Inu mulibe Moyo uliwonse apobe, chifukwa inu munatenga dzina lolakwika. Koma ndinu—ndinu . . . bolako inu mwalanditsidwako. Mwaona, inu muli . . . inu—inu mwathawa mpingo wa Roma. Inu mwathawa mbalume zonse zimenezo, ndipo inu bola mwatuluka patali chonchi.” Tsopano, inu mukuwerenga Baibulo lomwelo. Tsopano, koma Baibulo lomwelo limene limaphunzitsa Mzimu Woyera . . . Iye sanawadzule iwo pa zomwe iwo anali nazo. Anati, “Tsopano ndizo . . . gwiritsitsani ku chimenecho mpaka Ine nditabwera. Mwaona, muzingogwiritsitsabe.”

<sup>141</sup> Tsopano, m'badwo wa mpingo unayamba pafupifupi mu 1520, pamene wa Roma, mpingo wa Katolika wa ponseponse unadzakhala ndi kukhazikika kwathunthu. Zimenezo zinakhalapo mpaka Okutobala sarte wani (Ngati inu nonse mukulemba zimenezo.) Okutobala sarte wani, 1570 A.D., pamene Martin Luther anadzakhoma mfundo yake yachi naintefaivi pakhomo la tchalitchi ku Wittenberg, Germany, ndipo kuyambira nthawi imeneyo Kukonzanso kunayambika. Kodi inu munalemba madeti amenewo? Ndiroleni ine ndibwerezense izo



kuti inu mukhale otsimikiza. Okutobala pa sarte-wani, 1570 A.D., pamene Martin Luther anakhoma mfundo yake yachi naintefaivi pakhomo la tchalitchi ku Wittenberg, W-i-t-t-e-n-b-u-r-g, Wittenberg, Germany. Kuyambira tsiku limenelo kukonzanso kunayambika, moto unayamba kuwuluzika. Iye anawutsutsa mpingo wa Katolika umenewo ataima pamenepo, izo mdzanja lake monga choncho, iye anati, "Ili lingakhale Thupi loyera la Khristu? Ndi kamkate ndi vinyo pang'ono!" Ndipo "phwaa!" iye anaziponyera izo pansi. Zoona zimenezo.

<sup>142</sup> Iye anawutsutsa mpingo wa Katolika, ndipo a...izo zinayamba...kulandidwa pang'ono kunabwerapo kenako. Chabwino, a...zinali zitayambika. Koma izo mochluluka zinali ku—kumenyera mphamvu za ndale kuposa momwe zinaliri kwa Mpingo woona, kwa miyezo ya Chikhristu. Iwo ankangomenyera ufulu wandale kuti atuluke mu mpingo ndi kukapanga mpingo wina. Iwo sanakonzedwe nkomwe, amatuluka mu mpingo wa Katolika kuti akabwezeretsenso Mzimu Woyera ndi mphamvu mu mpingo, chifukwa iwo anawukana Iwo. Huh? Uwo unali msonkhano wandale. Ndiko kumene izo zikanakwanirako ndithudi, "Iwe uli nalo dzina kuti uli moyo, ndipo ndiwe wakufa." Mwakulankhula kwina, iye anangotulutsako chipembedzo cha Chiprotestanti, ndizo zonse. Iye anabweretsako mwana wamkazi kuchokera mtchalitchi. Kuchokera mu...Iye anabweretsako wachiwerewere kuchokera mwa hule. Ndizo ndendende zomwe zinali zitachitika. Iye anabweretsa Ataliya kuchokera mwa Yezebeli.

<sup>143</sup> Tsopano, aliyense amene amawerenga Kukonzanso akudziwa kuti ndi choncho, chifukwa iye basi mophweka... Zotsalira zapang'ono zakale ndi kachitidwe kamene...ndi miyambo, iye—iye mophweka anangozigwetsa izo, koma pona za kubwezeretsa Mzimu Woyera mu mpingo monga momwe zinkakhalira kumbuyo *uku*, iye sanachite izo. Ayi, bwana. Iyo inali nkhondo yandale kuposa momwe iyo inaliri nkhondo yauzimu. Izo zinali zandale mmalo mwa Mzimu Woyera. Iye anali asanalowebe mu Mpingo. Oh, m'bale, Iye anali asanabwerere; Iye akubwerera *apa*, osati pamtunda *apo*.

<sup>144</sup> Tsopano, kunali kusonkhana kwakukulu kwandale, koma iko sikunali kwa Malemba Oyera ndi—ndi Mzimu Woyera. Unali msonkhano wandale mwakuti iye anachotsapo zina za zotsalira zakale za pamtanda, ndi a "*Tikuoneni Maria*," ndi zonse izo. Koma iye anabweretsabe katekisimu. Iye anabweretsabe izi... Inu mumadzitcha izo chiyani? Misonkhano yodzipereka ya chirichonse chomwe chinali kumusi uko pamene iwo amapita uko mmawa wa Isitara ndipo abusa amawafunira iwo "Khrisimasi yabwino," inu mukudziwa. "Osaziwonanso izo mpaka nthawi ya Khrisimasi," iye anati, inu mukudziwa. Zimenezo...oh, kutsimikizira—kutsimikizira ntchitoyo, zomwe ine ndikuyesera kuti ndinene. Zigwetsereni izo

pansi ndipo atsimikizireni iwo, adyetseni iwo mgonero woyamba ndipo muwatsimikizire iwo. Kulibeko chinthu choterocho chotchedwa kutsimikizira. Kutsimikizira kokhako kumene kumatchulidwa mu Baibulo, pamene mu—mu Baibulo, ndi pamene Mulungu anatsimikizira Mawu Ake ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zikutsatira. Kumeneko ndiko kutsimikizira, osati kutsimikizira kuti ndiwe wa mpingo wa Lutheran, koma Mulungu kutsimikizira Mawu Ake mwa iwe. “Ndipo Ambuye anali...anagwira nawo ntchito,” Marko 16, “akutsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikuwatsatira.” Ndiko kutsimikizira kwa Mpingo wa chipentekoste. Ndiko kutsimikizira...Mulungu amadzitsimikizira Yekha wamoyo, ngati Mulungu wochita zozizwitsa mu Mpingo, kuyankhula mmalirime, kutanthauzira kwa malirime, ndi kumachita zinthu zomwe zomwezo zomwe iwo ankachita pachiyambi.

<sup>145</sup> Kodi ine ndikukutopetsani inu? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Chabwino. Tsopano, zindikirani, iwo sanabweretsenso chitsitsimutso cha Mzimu Woyera; iwo anabweretsanso m’badwo wa mpingo watsopano. Iwo anabweretsanso yemwe analandidwayo; wopulumukayo ku ulamuliro wolowezana wa Chiroma, kuti akapange ulamuliro wolowezana wa Chiprotestanti. Ndicho chinthu chokhacho chimene iwo anachita. Analumphu kuchokera mu chiwaya kupita pamoto, mwawona. Izo—ndiko kulondola. Ndendende.

<sup>146</sup> Yezebeli anangobereka mwana wamkazi. Ndipo tsopano musaganize kuti ine ndikungonena izi kuti—kuti ndiwoneke wanzeru, ine ndikunena izi chifukwa Baibulo linanena chomwecho! Baibulo, mu Chivumbulutso 17, linati, “Iye anali mayi wa timahule.” Yesu ananena apa, “Monga momwe Yezebeli analiri, chomwecho iye adzakhala.” Ndipo iye anabereka ana aakazi amene anaipitsa dzi—dziko limene linali losaipitsidwa. Tsopano, ndizo ndendende zomwe Chiprotestanti chinachita kwa Mzimu weniweni wa Mulungu, icho chinaipitsa chinthucho ndipo chinachiyikanso icho kubwerera mu bungwe lina. Chimene, ngati Mulungu alola, Lamlungu mmawa, ine ndikufuna ndidzakuwonetseni inu kuti—kuti—kuti iwo akupanga fano kwa chirombo, ndipo chirombocho chinali Roma. Ndipo iwo anapanga fano *ngati* limenelo. Chinali chiyani icho? Bungwe! Oh, ine ndikuyembekeza kuti zimenezo zikulowerera pansu mmitima ya anthu.

<sup>147</sup> Ndipo inu mumadabwa chifukwa chimene ine ndakhala ndikulimbana ndi bungwe mwamphamvu moyo wanga wonse; ine sindimadziwa inemwini. Koma Icho chinali *Chinachake* mkati mwanga chikulirira; ine sindikanachitira mwina. Ine ndimadabwa, nthawizonse ndimadabwa, nchifukwa chiyani ine nthawizonse ndimatsutsana ndi akazi chomwecho? Mukuona? Moyo wanga wonse. Osati chi-...ine ndikutanthauza... sindikutanthauza akazi enieni; Ine ndikutanthauza awa *amene*

*amayenera kukhala*, inu mukudziwa, minyewa ya chikhaliidwe inaduka kutuluka mwa iwo ndi chirichonse. Inu mukudziwa. Ndiwo mtundu womwe ine. . . *Chinachake* mwa ine.

<sup>148</sup> Pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, wochepa, mnyamata wakale, kumtunda uko, ine ndimakhoza kuwawona akazi amenewo akubwera uko pa msewu, ndi zawo. . . ndimadziwa kuti amuna awo ali ku ntchito, iwo ali kumtunda uko ndi mnyamata wina, ataledzera; mmphepete mwa msewu, ndipo iwo amakhoza kumawayendetsa iwo chokwera ndi chotsika mu msewu, kuwakhazikitsa bwinoko iwo mokwanira kuti akafike kunyumba, kukawaphikira chakudya chamadzulo amuna awo. Ine ndinati iwo si oyenera chipolopolo choyera kuti chidutse mwa iwo. Uko nkulondola. Ine ndinati iwo ndiwotsika kuposa nyama, omwe angachite chinthu ngati chimenecho. Ndipo ine. . . Pamene ine ndinali ndi usinkhu wa zaka seventini, eyitini ine ndimakhoza kuwona mtsi—mitsikana akubwera akutsika msewu, Ine ndimakhoza kuwolokera tsidya linalo, ine ndinkati, “Mphiri yonunkha imeneyo.” Mukuona? Ndipo ine ndikanakhala wodana nawo weniweni, koma pamene ine ndinalandira Mulungu mumtima mwanga, Mulungu anandidziwitsa ine kuti Iye ali nazo ngale zina kunjira uko, Iye ali nawo madona enieni. Iwo onse sangadziditse okha monga choncho; ndikuthokoza Mulungu chifukwa cha zimenezo.

<sup>149</sup> Pamene ine ndinali uko ku Africa, pamene ine ndinali uko ku Switzerland, komanso pamene ine ndinali ku Roma, ine ndimafunsiidwa funso ili kwambiri, “Hei, nenani, M'bale Branham, kodi inu nonse mulibe akazi abwino nkomwe mu Amereka? Nyimbo iliyonse imene imabwera kuno, pamakhala chinachake chachidetsa chokhudza akazi anu.”

<sup>150</sup> Ine ndinati, “Amenewo ndiwo Achimereka. Koma ife tiri ndi Ufumu wina uliko kumeneko, umenewo ndiwo Ufumu wa Mulungu; aliko madona enieni.” Iwo aliko!

<sup>151</sup> Baibulo linatero, umo mu—mwa aneneri, anati. . . Ine ndikukhulupirira izo zinali pafupifupi mutu wa 5 wa Yesaya, Ine sindikutsimikiza, izo zingakhale mu mutu wa 5 kapena mutu wa 6 pamenepo; kuyankhula za, “Wodala ndi mwana wamkazi uja wa Zioni, adzapulumuka mu tsiku limenero kuchoka ku zinthu zonsezo.” Momwe iye angayendere mu msewu; iye amakokera masokosi ake pansu; iye amazithyolathyola akamayenda; kuthimbwidzika monga choncho, ndi zinthu zomwe iye amazichita. Ndendende basi momwe iwo amachitira tsopano, mwangwirowo basi. Kuvala zovala ngati mwamuna, zomwe ndi zonyansa kwa Mulungu.

<sup>152</sup> Ine ndinawona gulu lachipembedzo, kanthawi kapitako, likupita kukakhala ndi. . . mtundu wina wa kuphulika komwe iwo amakhala nako usiku uliwonse, ndipo akazi awa onse akupitako atavala zimakabudula izi-. . . Kapena—kapena

chiyani—kapena kodi ndi chiyani zinthu zimenezo chimene inu mumazitcha izo? Osati makabudula, koma zinthu zinazo. Eya, iyo ndi zimitemwende. Kapena zinthu zimenezo pamenepo. Zonse pa...Iwo amafuna tharauza lopindidwa, chabwino; m'bale, limenelo ndi bolodi lalikulu *choncho*. Uko nkulondola. *Mutu* umachokera *woyenda pansi*, ndizo “pa phazi lako,” ndipo ndizo ndendende zomwe iwo amafuna. Uko nkulondola.

153 Koma, oh, inu mukuti, “Chabwino, tsopano, ine ndikuganiza kuti ndi cha ulemu kwambiri kuti mkazi azivala zimenezo kuposa siketi.”

154 Mulungu anati, “Ndi chonyansa pamaso Pake kuti mkazi azivala chovala. . .” Ndipo pamene mkazi adula tsitsi lake ngati mwamuna. . .Mulungu amafuna kuti mkazi aziwoneka ngati mkazi, azivala monga mkazi, azichita monga mkazi.

155 Ndipo Iye samafuna mwamuna wokhala ndi zindevu zolendewera zambiri mmasaya monga *chonchi*, ndiyeno, monga bakha atakhala kumbuyo kwa mutu wake monga *choncho*. Iye amafuna kuti iye aziwoneka ngati mwamuna. Inde, bwana. Mai, iwo amavala zachikazi mpaka iwo samadziwa nkomwe kuti iwo ndi mwamuna kapena mkazi. Ndi—ndi zomvetsa chisoni, a zakezokha awa ndi chirichonse zomwe ife tiri nazo lero. Nzosadabwitsa kuti ife tikukhala mu nthawi yotsiriza, palibe chimene chatsalira mdziko lino koma kuti Mulungu atsanulire mkwiyo Wake pa ilo ndi kuliwotcha ilo. Ndizo zonse. Mulungu wolungama ndi Woyera sangachitenso china chirichonse.

156 Iwo akana Magazi a Yesu Khristu! Iwo adziphunzitsa mbalume okha! Iwo alowa mu bungwe! Ndipo wakale . . . bambo wina woyera wakale ali ndi yake. . . batchala yakale ndi kolala yake yotembenezidwa, kubwerapo ndi kudzawawuza iwo, “Ana anga odala.” Izo sizikutanthauza chirichonse koma nkumba yaikazi ikunena izo.

157 Ine ndikukuuzani inu, chimene ife tikusowa usikuuno ndi kubwerera ku Baibulo ndi Mzimu Woyera, m'bale, ndi mphamvu ya Khristu woukitsidwayo ikubwera mu Mpingo kumadzachita zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa. Ameni! Ndiwo Uthenga. Inde.

158 Kubweretsapo. . . chotero. . . Inde, uko nkulondola, izo zinatero. Chi—chi—chitsitsimutso chinachita zinthu zina zabwino kwambiri kumeneko, chitsitsimutso chimenecho. Koma icho sichinabweretseko Mzimu Woyera. Iwo sanabweretsepo zimenezo mpaka kutsika mu m'badwo wa Laodikaya uwu, kutsika mu m'badwo wa Chipentekoste. Koma icho chinachita chinthu chimodzi. Chitsitsimutso ichi chinachita zinthu zina zomwe Iye ananena, “Musalole kuti izo zife tsopano, zilibikitseni ndipo mupitirize kuwonjezera kwa izo.” Mukuona?

159 Icho chinabweretsapo Baibulo laulere kwa anthu kenanso. M'badwo wa Chilutera unabweretsa Baibulo laulere. Iwo anapanga makina awo osindikizira ndipo anayamba kumapereka kwa dziko lapansi Baibulo. Mulungu awadalitse Achilutera pa zimenezo! Inde, bwana. Anabwezeretsanso Baibulo kubwerera mdzanja la anthu wamba kenanso; anali wansembe yekha. Samayerekeza ngakhale kuti ayang'ane pa Ilo; chifukwa zinali zimene papa wanena, ndipo iye anali mulungu; koto chirichonse chimene iye wananena, icho chinkachita izo.

160 Chotero tsopano, chitsitsimutso cha Chilutera, chimene iwo ankafuna, kuti “achilimbikitse.” Tsopano inu muli ndi Baibulo mdzanja lanu, tsopano kawerengeni Ilo! Mukakhulupirire Ilo! Musati mukaliike Ilo pa alumali, ndikuti, “Chabwino, ife tiri ndi Baibulo.” Izo sizikakuchitirani inu ubwino kumeneko. Alipo Achilutera ambiri mu Pentekoste lero, amalisiya Baibulo pamene ndi kumatenga zomwe winawake akunena za Ilo. M'bale, muziwerenga Mawu! “Muzifufuza Malemba, pakuti ndi iwowo amene amachitira umboni za Ine,” anatero Yesu. “Mmenemo inu mumaganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya.” Ndicho chinthu choti muzichita: muziwerenga Mawu!

161 Tsopano, Iye ananena kuti, “Azingogwiritsitsa kwa Iwo, a...musati—musalole kuti izo zikutayikeni.” Ndipo chinthu china chimene Iye ankafuna kuti iwo agwiritsitseko, iwo anali nayo mphamvu pang'ono itatsalira mwa iwo, inali...Chitsitsimutso cha Chilutera, chinthu chachiwiri chimene icho chinachita, icho chinabweretsa chiphunzitsa cha kulungamitsidwa ku kuwala. Akatolika samatenga kulungamitsidwa; ndi mpingo wa Katolika.

162 Chimodzimidzi monga wansembe uja, iwo anachita kumuchotsa iye pa wailesi kuno nthawi ina mmbuyomu. Iye anati, “Kulibeko chipulumutso china kulikonseko koma mu mpingo wa Katolika.” Chipulumutso chiri mwa Khristu; osati mu mpingo wa Katolika, osati mu mpingo wa Chiprotestanti. Chiri mwa Khristu, chipulumutso. Koma Akatolika amakhulupirira...Iwo samasamala zomwe Baibulo limanena; ndi zimene mpingo umanena. Mukuona? Inu simungathe kuyankhula ndi iwo, chifukwa palibepo njira—palibepo njira yoti ungayankhulirane ndi iwo. Iwo samasamala. Iwo ali nawo...Iwo amayankhula nawe iwe pa katekisimu wawo, chirichonse chonga zimenezo; koma inu mukabwera ku Baibulo, iwo—iwo amangolitaya Ilo, “Ndi zimene mpingo umanena.”

163 Koma Yesu anati, mu chinthu chomwechi, Yesu Mwiniwake anati, “Ngati munthu aliyense adzachotsa kalikonse kapena kudzawonjezera kalikonse kwa Ilo, Iye adzamchotsera gawo lake mu Bukhu la Moyo.” Yesu anati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale Choonadi. Miyamba

ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita konse.” Nkulondola uko? Oh, Ndi zimenezotu, m’bale.

<sup>164</sup> Ndine wokhulupirira mu Mawu a Mulungu! Uko nkulondola. Ndipo osati Mawu okhawa amene Mulungu akuyankhula *pamenepo*, ndiye ine ndinawapempha Atate Akumwamba kuti andipatse ine Mzimu Woyera kuti *atsimikizire* Mawu amenewo, kuti apangitse Khristu azikhala moyo mwa ine. Kuti ine ndizidziwa kuti ine ndiri nawo Moyo Wamuyaya, osati chifukwa chakuti ine ndikuyenera Iwo, chifukwa chisomo Chake chapereka Iwo kwa ine. Ndiro thanthwe. “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga,” Iye anatero.

<sup>165</sup> Chabwino, kulungamitsidwa. Chabwino. Nkhani yake inali yakuti, iwo atabweretsapo kale chinachake chomwe iwo samayenera kuchilola kuti chife, chimenecho chinali, iwo anali atatenga Baibulo mdzanja lawo kachiwiri. Achilutera anachita zimenezo. Ndipo chinthu china, iwo ali nacho chiphunzitso cha “kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro.” Ndizo zomwe Luther ankaphunzitsa, aliyense akudziwa kuti chimenecho chinali chiphunzitso chake. Kulunga-. . . Kodi inu simukuwona momwe izo ziliri zangwiwo? Ndiye motsatira kunadza Wesley ndi kuyeretsedwa, ndiye apa pakudzabwera Chipentekoste ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwangwiwo basi. Tsopano ine. . .

<sup>166</sup> “Inu muli nazo zinthu zingapo, gwiritsitsani kwa izo tsopano, ndipo—ndipo musalole kuti izo zife. Ngati inu simugwiritsitsa kwa izo, Ine ndidzabwera msanga ngati mbala ndipo inu mudzabwereranso kupita ku chipembedzo kachiwiri.” Ndipo ndizo zimene iwo anadzachita, chimodzimodzi basi, anabwereranso mmbuyo. “Inu mubwereranso kumene kwa Chinikolai kachiwiri, chifukwa inu mudzabwereranso konko ku chipembedzo. Gwiritsitsani! Kazipitirizani kumawerenga Baibulo limenero, ndi kupitirira kulungamitsidwa, ndi kupitirira kumakanikizabe.” Koma pali wotsalira wapang’ono omwe anadzatuluka mmenemo. Otsalira apang’ono.

<sup>167</sup> Patadutsa, kubwera koyamba, Luther; kenako kunadzabwera Zwingli; mpaka mmusi, Calvin; ndi kumapitirira, ndi zina zotero, mpaka mmusi kwa Wesley. Koma panali wotsalira wapang’ono amene anadzatuluka kumeneko amene ankaphunzitsa kuyeretsedwa. Ndipo kuchokera mu kuyeretsedwa kunadzabwera wotsalira wapang’ono amene anapitirira kukalowa mu Mzimu Woyera. Mwaona, wotsalira wapang’ono ameneyo, njira yonse motsatira pamenepo, akusunga Icho—Icho chamoyo. Chabwino.

<sup>168</sup> Koma, chachitatu, iwo anabweretsako mitundu yambiri yachipembedzo chachikunja ndi iwo, limodzi ndi izo, monga ngati zipembedzo, ubatizo wabodza. Tsopano, iwo anatulukako akukonkha ndi zina zotero monga choncho, ndi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Iwo anabweretsako katekisimu. Zoonadi

anali nazo. . . zoonadi iwo anagwirizana bwino ndi dzinalo. . . ndi. . . zomwe Yesu ananena apa, “Inu muli ndi dzina kuti ndinu amoyo, koma ndinu akufa.” Uko nkulondola. Chabwino.

<sup>169</sup> Chachinai, izo nzoona kuti kukonzanso kunasesa zotsalira zawo zambiri zopukutidwa ndi—ndi miyambo ndi zina zotero, koma izo zinalephera mu mpingo ndi kubwezeretsa kwa kubweretsa kukonzanso, izo zinalephera kubwezeretsanso chiphunzitso cha Uthenga wathunthu wokhala ndi zizindikiro zikutsatira. Mpingo wa Chilutera sunakhale nazo konse izo. Iwo sanakhale nazo konse izo; ndipo iwo sanakhale nazo konse izo mu m'badwo wa Chiwesile. Iwo anangokhala nazo izo kumapeto kwa m'badwo uwu wa Laodikaya.

<sup>170</sup> Tsopano, pamene ife tidzafike mu zimenezo, ife tidzawerera kumene mu Malemba ndi kudzakuwonetsani inu ndendende basi momwe iwo analonjezera izo. Iwo analibe. . . sanabwezeretse chitsitsimutso cha Mzimu Woyera.

<sup>171</sup> Iwo anachoka ku mafano; ndipo iwo anapotoloka kusiya mafano, izo nzoona. Iwo anagwetsera pansi mafano kuwachotsa mu tchalitchi: Maria, ndi Yosefe, ndi—ndi Petro, ndi Paulo, ndi onsewo. Iwo anachoka ku mafano, koma iwo sanatembenukire kwa Khristu woukitsidwayo. Luther anawachotsa iwo ku mafano, koma zinali mochuluka ngati ndale kapena a—kapena chipembedzo kapena bungwe, kuti akadzipangire okha bungwe lina (fano longa loyambalo) ndi kuyesera kuliposa ilo ndi chipembedzo.

<sup>172</sup> Ndipo tsopano iwo akumenyanabe. Amethodisti akufunabe kutero. . . Abaptisti onse kuti akhale Amethodisti. Ndipo Achilutera onse amafuna Abaptisti onse ndi Amethodisti akhale Achilutera. Achipentekoste amafuna Abaptisti onse, Achilutera, ndi china chirichonse, kuti akhale Achipentekoste. Mwaona, inu muzingopitira kumawonjezera ku chipembedzo chanu. Koma limenelo sindiro dongosolo la Mulungu kuyamba ndi kuyamba. Dongosolo la Mulungula kubwezeretsa linali loti abwezeretse zomwe zinalipo kuyambira pachiyambi.

<sup>173</sup> Taonani! Kuwukitsa zimenezo! Ngati bukhu ili ligwera pansi, tsopano kutenga bukhu lina ndi kulilowetsa pa malo ake sikubwezeretsa, chiwukitsiro. Inu muyenera kubwezeretsapo *lomwelo* pamenepo. Ameni. Chotero ngati mpingo unafa kudutsa mu M'badwo wa Mdima ndipo unadzakhala chikunja kwathunthu kumbuyo *kuno*, ndiye kubwezeretsa, a. . . Kumeneko ndi kukonzanso, kukonzanso; koma kukonzedwanso, ndi *kubadwa kachiwiri*, ndi zinthu ziwiri zosiyana. Mukuona? Iwo anabwezeretsanso kukonzanso, kukonzanso, kuchoka ku ambiri a mafano awo ndi zina zotero, koma iwo sanawubweretse konse Mzimu Woyera kuti ubwerere mu mpingo. Oh, lidalitsike Dzina la Ambuye! M'bale, mlongo, kodi inu mukukhoza kuziwona izo? Iwo sanabwezeretse konse Mzimu Woyera, chifukwa

mmodzi amene amabweretsa kwenikweni Kuwala kowona kwa Uthenga . . . Valani chipewa chanu tsopano. Yemwe amabweretsa Kuwala kowona kwa Uthenga ndi mngelo wa mpingo kumusi *kuno*. Tsopano, ife tidzawona zimenezo Lamlungu.

<sup>174</sup> Tsopano, iwo adzakhala ndi kuwala pamwamba pa kuwala, ndi kuwala kwa Chikhristu, koma aliyense adzabwereranso kubwerera ku bungwe limenelo. Koma adzabwera wina amene adzaima motsutsana naye iye. Inde, bwana. Ndipo iye adzangwedeza wotsalira kuchokera kumeneko motsimikiza basi monga ine ndikuima pa guwa ili. Uko nkulondola. Ndipo iye adzapita kubwerera molunjika kupita kuchiyambi. Ndipo ine ndidzatenga Malemba kuchokera mu Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano ndi kudzakutitimikizirani inu kuti iye adzachita zimenezo, mngelo wa mpingo wa Laodikaya, ndiko kulondola, adzapita molunjika kubwerera kuchiyambi ndipo adzachiukitsa chinthu ichi kuno kachiwiri. Ndipo chiukitsiro chidzabwera pa tsiku la izi *apa*. Uko nkulondola.

<sup>175</sup> Koma Luther anawugwedezera mpingo kunjja, wopulumukayo. Wopulumuka *ameneyo*, sitepe imodzi, kuyere- . . . kulungamitsidwa. Wopulumukayo, iye anapeza ndi phazi limodzi kutuluka kuchikunjja. Izo zonse nzabwino. Nthawi yotsatira, adzatuluka ndi mapazi awiri. Ndizo zonse.

<sup>176</sup> Monga ngati . . . Kodi inu munazindikira mu Baibulo kuti pali—pali madzi akutuluka kuchokera kuseri kwa Kachisi? Ndipo iye anati iye anawona madzi mpaka mmaondo ake; kenako chotsatira, madzi mpaka mchiuno mwake; ndipo nthawi yotsatira, iwo anadutsa pamutu pake. Koma pamene iwo anadutsa pamutu pake, iye amayenera kufika pamalo omwe iye akanatha kusambira. Mwaona, iye ankayenera kuti azisambira.

<sup>177</sup> Chotero ife tikufika pamalo tsopano amene mwina tisambira kapena timira. Ndizo zonse. Iwo adzakumizani inu ndi kukuthamangitsirani inu kutali kwathunthu, kapena kukubweretsani inu mkati, chimodzi. Chotero, ndi kusambira kapena kumira! Aleluya! Oh, ndine wokondwa kwambiri ndi Mzimu Woyera! Sichoncho inu?

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti  
ndine mmodzi wawo.

Ndine mmodzi wawo . . . (Nchiyani *ivo*? Osati  
*ichi*, *icho*, kapena *icho*, kapena *icho*.)  
. . . wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wawo; (Aleluya!)

Mmodzi wawo, mmodzi wawo,  
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena kuti  
ndine mmodzi wawo.

Kodi zimenezo sizikumveka bwino? Mvetserani:



Anasonkhana mchipinda chapamwamba,  
 Onse akupemphera mu Dzina Lake,  
 Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,  
 Ndipo mphamvu ya ntchito inabwera;  
 Tsopano chimene Iye anachita kwa iwo tsiku  
 limenero  
 Iye achita kwa inu chomwecho,  
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
 mmodzi wawo.

Oh, mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,  
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
 mmodzi wawo; (Aleluya!)  
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo,  
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
 mmodzi wawo.

<sup>178</sup> Kodi iwo amapita ku maseminare? Ayi. Ena a iwo sangathe ngakhale kulemba dzina lawo. Uko nkulondola. Petro sankatha. Baibulo linati iye anali mbuli ndi munthu wosaphunzira, iye ndi Yohane. Koma iwo ankayenera kuti awamvere iwo, chifukwa iwo ankadziwa kuti iwo amakhala ali ndi Yesu.

Ngakhale anthuwa sangakhale ophunzira  
 (Ophunzitsidwa.),  
 Kapena kunyadira kutchuka kwadziko (“Oh,  
 Mulungu adalitsike, ine ndiri nawo ochuluka  
 kwambiri *akuti-ndi-akuti*.”),  
 Onse alandira Pentekoste wawo,  
 Anabatizidwa mu Dzina la Yesu;  
 Ndipo iwo akunena tsopano, kutali ndi  
 motalika,  
 Mphamvu Yake ndi yomweyo,  
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
 mmodzi wawo.

Oh, mmodzi wawo, mmodzi wawo,  
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
 mmodzi wawo;  
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo,  
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
 mmodzi wawo.

<sup>179</sup> Kodi sindinu okondwera ndi zimenezo? Wokondwera kwambiri kukhala mmodzi wawo. Ine kulibwino ndikhale mmodzi wawo kuposa chirichonse chimene ine ndikuchidziwa. Oh, ine kulibwino ndikhale mmodzi wawo kuposa kukhala Purezidenti wa United States kapena kukhala mfumu padziko lonse lapansi. Ine . . . Ngati Ambuye Yesu akanayenda pansu apa, ndikuti, “Ine ndikubwezeretsa iwe kukakhala wa usinkhu wa zaka twente ndipo ndikakupanga iwe kukhala woyang'anira, mfumu ya dziko lonse, ndipo ndikakupatsa iwe zaka teni

sauzande za—za moyo pa dziko lapansi ili, kuti udzakhale usinkhu wa zaka twente; osadzakhala konse ndi tsiku lodwala, kupweteka mtima, ndipo zonse zidzakhala chisangalalo ndi chirichonse, ndi mfumu ya dziko lonse, nkudzakhala moyo zaka teni sauzande; kapena kodi inu mungafune kukhala mmodzi wa iwo ndi kumangovutikira monga momwe inu mukuchitiramu?”

<sup>180</sup> Ine ndinganene kuti, “Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine mmodzi wawo!” Zitatha zaka teni sauzande, kenako chiyani? Koma Uku ndi Kwamuyaya. Kodi Iwo unabwera motani, m’bale? Oh, Izo zakhala zikudutsa mu Magazi. Uko nkulondola. Izo zabwera mtunda wautali, ndipo Izo zinabwera ndi Mulungu atapangidwa thupi ndi kudzakhala pakati pathu:

Modyetsera ng’ombe kale, izi ndi zoonā,  
Mwana anabadwa kudzapulumutsa anthu ku  
machimo awo.

Yohane anamuwona Iye pa gombe,  
Mwanawankhosa kwa nthawizonse,  
Oh, Khristu, Wopachikidwa pa Kalvare.

Oh, ndimkonda Mwamuna waku Galileya,  
waku Galileya,

Poti Iye anandichitira zambiri.

Wandikhululukira machimo anga onse,  
anandipatsa Mzimu Woyera;

Oh, ndinkonda, ndinkonda Mwamuna waku  
Galileya.

Mkazi wa pa chitsime, Iye anamuuzā machimo  
ake onse, (Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi  
kwanthawizonse.)

Ndipo momwe iye anali ndi amuna asanu pa  
nthawi imeneyo.

Anakhululukidwa tchimo lake lonse, ndipo  
mtendere wozama unadzamo;

Anafuula, “Bwerani mudzawone Mwamuna  
waku Galileya!”

Oh, ndimkonda Mwamuna waku Galileya,  
waku Galileya,

Poti Iye anandichitira zambiri.

Wandikhululukira machimo anga onse,  
anandipatsa Mzimu Woyera;

Oh, ndimkonda, ndimkonda Mwamuna waku  
Galileya.

Wamisonkho popemphera tsiku lina mkachisi,  
Analira, “O Ambuye, mundichitire chifundo!”

Anamukhululukira tchimo, mtendere wozama  
unadzamo;

Anati, “Bwerani mudzaone Mwamuna waku  
Galileya.”

Ine ndikuzikonda zimenezo. Sichoncho inu?

Wolumala anayenda, wosayankhula  
 anayankhula,  
 Mphamvu ija inayankhula ndi chikondi pa  
 nyanja;  
 Ndipo wakhungu anawona, ndikudziwa  
 zikanangoyenera kukhala  
 Chifundo cha Bambo uja wa ku Galileya.

Muyimbe iyo ndi ine:

Oh, ndinkonda Mwamuna wa ku Galileya, wa  
 ku Galileya,  
 Poti Iye anandichitira zambiri ine.  
 Wandikhululukira machimo anga onse,  
 nandipatsa Mzimu Woyera;  
 Oh, ndinkonda, ndinkonda Mwamuna wa ku  
 Galileya.

<sup>181</sup> Kodi inu simukuzikonda Izo? Oh, mai! Uthenga wabwino uwu, wa Mzimu Woyera, oh, momwe ine ndimawukondera Iwo. Ine ndimankonda Iye ndi mtima wanga wonse. Ndipo ndine wokondwa kwambiri usikuuno kuti ine ndikuwerengedwa ndi iwo, ndipo ife tiri limodzi ngati abale ndi alongo. Abaptisti, Amethodisti, Pres-. . . Akatolika, Apresbateria, china chirichonse, Mulungu watibweretsa ife kuchokera mmayendedwe onse amoyo ndipo watibweretsa ife kuno ku chiyanjano chachikulu ichi cha Mzimu Woyera. Osati kukhala a chipembezdo chirichonse, izo ziri ndi iwo zimene iwo akuchita, koma ife tiri mu Ufumu wachinsinsi. Ife tinabatizidwa kulowa mu thupi lachinsinsi la Yesu Khristu, mwa Mzimu Woyera. Ndi ndani? Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, ndi aliyense amene akufuna, muloleni iye abwere.

<sup>182</sup> Yesu anati, “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo palibe mmodzi wa iwo adzataike, ndipo Ine ndidzawaukitsa iwo pa tsiku lotsiriza.” Oh, mai! Ife tinkakonda kuimba nyimbo yakale kumusi pa guwa kuno; sitikudziwa ngati ife tingaiyimbe iyo kapena ayi, “Malo, malo, inde, alipo malo, alipo malo pa kasupe a ine.” Inu mumazikonda nyimbo zakale zimenezo monga choncho? Tipatseni ife kiyi winawake, winawake amene amadziwa kuyambitsa kwake. Kodi walimba wathu ali kuti? Kodi iye ali pano? Kapena M'bale Teddy kapena aliyense wa iwo pano? Iwo? Oh, mai, ine—ine sindikumuwona iye paliponse.

Malo, malo, inde, alipo malo,  
 Alipo malo pa Kasupe a inu;  
 Malo, malo, inde, alipo malo,  
 Alipo malo pa Kasupe a inu.

<sup>183</sup> Inu mumazikonda nyimbo zakale zimenezo? Ndipo ine ndimaikondanso iyi nayonso:

Pansi pa mtanda pamene Mpulumutsi anafa,  
 Pansi apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;  
 Oh, apo pa mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa Dzina Lake!

Ulemelero kwa Dzina Lake! (Dzina Lake  
 lofunika!)

Oh, ulemelero kwa . . .

Tiyeni tingotseka maso athu tsopano ndikuiyimba iyo.

Oh, apo pa mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa Dzina Lake!

Ndapulumutsidwa modabwitsa ku tchimo,  
 Yesu mokoma akukhala mkatimu,  
 Pa mtanda Iye anandilowetsamo;  
 Ulemelero kwa Dzina Lake!

Ulemelero kwa Dzina Lake! (Dzina lofunika  
 limenelo!)

Ulemelero kwa Dzina Lake! (Dzina Lofunika!)  
 Apo pa mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa Dzina Lake!

<sup>184</sup> Tsopano pamene ife tikuimba ndime yotsatira iyi, gwiranani chanza ndi winawake patsogolo panu, kumbuyo kwanu, mmbali mwanu.

Bwerani, ku Kasupe uyu wolemera ndi  
 wokoma;

Ponyera moyo wako wosauka pamapazi a  
 Mpulumutsi;

Oh, gweramo lero, ndipo ukhale  
 wamphumphu;

Ulemelero kwa Dzina Lake!

Ulemelero kwa Dzina Lake! (Dzina lofunika  
 limenelo!)

Ulemelero kwa Dzina Lake lofunika!  
 Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa Dzina Lake!

Oh, ine ndimaikonda imeneyo. Sichoncho inu?

Ulemelero kwa Dzina Lake! (Dzina Lofunika!)  
 Ulemelero kwa dzina Lake!

Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa dzina Lake!

<sup>185</sup> Oh, mai! Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha zimenezo. Sichoncho inu? Wokondwa kwambiri kuti ine ndikhoza kubwera pa Kasupe uyu wolemera ndi wokoma kwambiri, ndikuponyeramo moyo wanga wosauka pamapazi a Mpulumutsi.

186 Ine ndikukumbukira tsiku lina, pamene ndinali mnyamata wamng'ono, wa pafupifupi usinkhu wa zaka eyitini zakubadwa, ndikuthawathawa kwa Ambuye. Ine ndinapita Kumadzulo, ine ndinkafuna. . . Abambo anga anali wokwera, ndipo ine ndinkafuna kupitako ndi kukathyola akavalo. Basi chinachake chikuchita njala mu mtima mwanga. Oh, ine ndikukuzani inu!

187 Ine ndinapita kwa mlaliki wa Baptisti, iye anati, "Imirira ndipo ungonena kuti, 'Yesu ndi Mwana wa Mulungu,' ife tikulemba dzina lako pa bukhu." Zimenezo sizinandikhutitse ine.

188 Kulikonse kumene ine ndimapita winawake. . . Seventh-day Adventist, ndinapita kukamuwona iye, munthu wabwino, M'bale Barker, m'bale wokondedwa, iye anati, "Billy, bwera ndipo udzavomereze sabata la Ambuye." (Ine ndiri nazo tsopano.) Koma iye anati, "Tsiku la sabata." Ndipo ine ndinaganiza, "Oh, mai, izo basi sizinachitebe izo." Inu mwawona.

189 Ine ndinapita Kumadzulo, ndipo ndinaganiza. . . Tinapita kumbuyo komwe uko usiku umenewo, ife tinali kokadyetsera ziweto. Ndipo, inu mukudziwa, inu munachotsa chishalo ndi chikwama chanu cha hema, ndi kuziyala izo, ndi kugwiritsa ntchito chishalo chanu ngati pilo. Ndipo ine ndinali nditatsamira kumbuyo, mmwamba pansu pa mitengo yakale ya paini iyo usiku umenewo. Ndipo ine ndinali pa ulonda wa masana, ndipo kotero anyamata ausiku anali panja akuzibweretsa ng'ombezo kumusi. Ndipo pamenepo panali mnyamata wachikulire wotchedwa "Slim," wochokera ku Texas, iye anali ndi—ndi gitala pamenepo ndipo iye anali akuimba:

Ulemelero kwa Dzina Lake!

190 Mnyamata wina kumeneko anali ndi chipeso ndi chidutswa cha pepala, akuwuzira mowomba pamenepo. [M'bale Branham akung'ung'uza, *Ulemelero kwa Dzina Lake—Mkonzi*]. Iwo anali akuyimba nyimbo zina, ma alakatuli oweta ng'ombe, ndipo anayamba kuyimba *Pansi pa Mtanda*.

191 Mai! Ine ndinatembuka, ndinadzayika bulangete langa pamutu panga monga *chonchi*. Ine ndinayang'ana mmbuyo uko, inu mukudziwa, ndipo zinkawoneka ngati nyenyezi zimenezo zinali zitapachikika pansu pamenepo pafupi ndi pamwamba pa mitengo imeneyo ndi mapiri amenewo. Kunong'ona kwamuyaya kwakale kwa mmapaini amenewo, ine ndimakhoza kumumva Iye akufuula, "Adam, iwe uli kuti?"

192 Pafupifupi masabata atatu zitachitika zimenezo, ine ndinapita kumusi mu mzinda ndipo anyamata onse anakaledzera, ndipo ine sindinkamwa. Ine ndimayenera kupita nawo onsewo kunyumba, kuwaunjika iwo mgalimoto, mulimonse. Ndipo iwo amapita kumeneko ndi kumawomberana pa zala za wina ndi mzake, ndi china chirichonse, ndi zowopsya

kuti ukhale wotetezeka; nkujambula mzere wolunjika ukutsika pamenepo, ndipo nkumabetcherana wina ndi mzake madola faivi ngati iwo angamayende pamenepo, ndipo iwo samakhoza kuyenda mmbali mwa msewu kunja uko monga choncho, inu mukudziwa. Ndipo umu ndi momwe izo zinaliri mpaka iwo onse atadzitolera, iwo atalandira ndalama zawo.

<sup>193</sup> Ndipo ine ndinali kumusi uko ndipo iwo onse anali akumwa, ine ndinapita kwinaku ndipo ndinakakhala pansi. Ine ndinaganiza, “Mai, mai!” Pafupifupi zaka sarte faivi zapitazo, kapena sarte faivi, ine ndikuganiza, zaka sarte faivi zapitazo. Ndipo ine ndinakakhala pansi pamenepo, pandekha. Phoenix anali malo aang’ono nthawi imeneyo, ife timachokera ku Wickenburg kumusi uko. Ine ndinali nditakhala pansi pamenepo, ndipo apo panali mtsikana wamng’ono wa Chispanishi akubwera akukupiza kudutsa pamenepo; ndipo ine nditakhala pamenepo ndi chipewa chachikulu ichi chitakhala kumbuyo pa mutu wanga; iye anadzadutsa apo ndipo anagwetsa mpango wawung’ono uwo, inu mukudziwa. Ine ndinati, “Hei, iwe wagwetsa mpango wako.” Ine ndinalibe nazo chidwi.

<sup>194</sup> Ine ndinamva phokoso pang’ono pansi mu msewu kumeneko, ndipo ndinapita kumusi kumeneko. Ndipo kumeneko kunali mnyamata wachikulire wotembenuzidwa kuchokera ku makola amenewo kunja uko, zizindikiro pankhope pake ponse, ndipo misozi ikutsikira mmasaya mwake pamenepo, akuimba gitala, akuyimba:

Ulemelero kwa dzina Lake!

<sup>195</sup> Oh, mai! Misozi ikutsika pankhope yake, iye anaima ndipo anati, “M’bale, iwe sungadziwe chomwe izo ziri mpaka iwe utalandira Khristu wodabwitsa uyu.”

Ulemelero kwa dzina Lake!

<sup>196</sup> Ndipo ine ndinakokera pansi chipewa chachikulu chija ndipo ine ndinapita kutali. Oh, mai! Iwe sungathe kubisala kwa Iye. Iwe ukhoza kungosokolokapo ndi kukamuvomereza Iye. Oh, Iye ndi wodabwitsa! Inde, Iye ali.

Ndapulumutsidwa modabwitsa ku uchimo,  
 Yesu mokoma kwambiri amakhala mkati,  
 (*Amakhala* mkati!)  
 Pa mtanda pomwe Iye ananditengera ine  
 mkati;  
 Ulemelero kwa dzina Lake!

Ulemelero kwa Dzina Lake! (Dzina!)  
 Ulemelero kwa dzina Lake!  
 Oh, pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa dzina Lake!

Oh, bwerani, ku Kasupe uyu wolemera  
 kwambiri ndi wokoma;  
 Ingoponyani moyo wanu wosauka pa mapazi a  
 Mpulumutsi;  
 Oh, gweramo lero, ndipo ukhale  
 wamphumphu;  
 Ulemelero kwa . . .

Tsopano tiyeni tiwera mitu yathu, ndikungokweza  
 manja athu tsopano:

Ulemelero kwa dzina Lake! (Ulemelero,  
 ulemelero!)

(O Mulungu!) (Dzina lofunika!)

Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;  
 Ulemelero kwa dzina Lake!

<sup>197</sup> Ulemelero kwa Mulungu! Tiyeni tiimirire. Oh, miniti yokha,  
 basi, dikirani.

[Mlongo akuyankhula mmalirime, m'bale akutanthauzira—  
 Mkonzi]. Inde, Ambuye.

<sup>198</sup> Tsopano ngati pangakhale ena omwe sangadziwe chomwe  
 icho chinali, ameneyo ndi Pentekoste, Mzimu Woyera  
 ukuyankhula. Yesu anati, “Pitani mdziko lonse, kalalikireni  
 Uthenga. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.  
 Iwo adzayankhula ndi malirime atsopano; adzayika manja pa  
 odwala, iwo adzachira.” Zinthu zonse izi zomwe Iye anazinena,  
 izo zidzafika pochitika.

<sup>199</sup> Oh, ndine wokondwa kwambiri. Kuwona Mzimu Woyera  
 ukubwera, kutsimikizira Mawu amenewo? Kuwala, tengani  
 zimenezo, musati—musakaikire izo. Ingolandirani izo ndipo Iye  
 adzachita ndi inu ngati mwana ndipo adzakubweretsani inu  
 pomwepo. Kodi uko sikukoma kwa Mzimu Woyera kuchita  
 zimenezo? Mzimu Woyera pa ife.

<sup>200</sup> Ine ndikukumbukira nthawi ina mu Baibulo, iwo  
 sankadziwa kuti chinthucho chikubwera kuchokera kuti, mdani  
 anali akubwera, ndipo Mzimu Woyera unadzagwera pa munthu  
 wonga ameneyo, ndipo unawauza iwo ndendende basi koti apite.  
 Ndipo iwo anapita kumeneko, ndipo Mulungu anasokoneza  
 ankhondo enawo ndipo anawayendetsa iwo. Uko nkulondola.

<sup>201</sup> Oh, tikukhalabe mmasiku a Baibulo, sichoncho ife? Ameni.  
 Nthawizonse, bola ngati Mzimu Woyera uli pamenepo.

<sup>202</sup> Oh, tiyeni tiime pamene tikuimba:

Tenga Dzina la Yesu . . .

Kumbukirani uthengawu.

Mwana wachisoni ndi watsoka;  
 Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
 Litenge Ilo kulikonse upita.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;

Dzina lofunika, (Dzina lofunika Ilo!) (Kukoma kwakeko!)

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

Tenga Dzina la Yesu limodzi nawe,

Monga Chishango ku msampha uliwonse;

Pamene mayesero akuzungulirani,

Pumani Dzina Loyeralo mu pemphero.

(Mulungu alemekezeke!)

Dzina Lofunika, O kukoma kwakeko!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

Mvetserani ku ndime imeneyo:

Tenga Dzina la Yesu limodzi nawe,

Monga Chishango ku msampha uliwonse;

Pamene mayesero akuzungulirani,

Pumani Dzina Loyeralo mu pemphero.

Oh, tiyeni tiyimbe iyo kachiwiri:

Tenga Dzina la Yesu limodzi nawe,

Monga Chishango ku msampha uliwonse;

Pamene mayesero akuzungulirani,

Pumani Dzina loyeralo mu pemphero.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano:

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;

Dzina lofunika, O kukoma kwakeko! (Kukoma kwakeko!)

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.





*M'BADWO WA MPINGO WA SARDE* CHA60-1209  
(The Sardisean Church Age)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachisanu madzulo, Disembala 9, 1960, ku Branham Tabernacle ku Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)